


# *Xodi Mzimu Woyera Unaperekedwera Chiyani?*

 Inu mukuona, M'bale Neville amakhulupirira mu kusanjika kwa manja. Ine ndawona ine ndiri nawo mafunso angapo. Tsopano, ine ndiwatenga awa mawa usiku, chifukwa ine ndiribe nthawi yoti ndiyang'ane pa iwo modutsa usikuuno, mwinamwake pa Uthenga wa usiku watha. Tsopano, ngati aliyense ali ndi funso pa uliwonse wa Uthenga, mudzangowayika iwo usiku umodzi, ndipo ine ndikhoza kudzawatenga iwo usiku wotsatira.

<sup>2</sup> Tsopano, mawa usiku ine ndikanafuna nditapeza, kapena kukhala nawo, kani, atumiki ena, ngati nkotheke; ngati sichoncho, ena abwino, amuna olimba kapena akazi omwe ife tingakhoze kuwayitana mu nthawi yofunika, kuti mu zochitika . . .

Mawa usiku ife tiyamba, ukatha Uthenga, kuti tisanjike manja, ndi, pofuna Mzimu Woyera. Ndiyeno, padzakhala . . . Inu muli nawo mwayi wanu wa kukhala pomwe pano ngati inu mukukhumba kutero, monse kupyola mu tchuthi, ngati izo zitenga motalika chomwecho kuti afe. Ndiyeno—ndiye, ngati sichoncho, ngati inu mukukhumba kuti mupite ku nyumba yanu komwe, bwanji, ife tikanakhala okondwa, ngati inu mungafike pa malo pamene inu . . . Basi simukudziwa koti mupite . . .

Ife tikufuna kuti mutenge atumiki ena, manambala awo, ngati iwo ali alendo; manambala awo, kumene iwo akukhala, kumene ife tingakhoze kuwapeza iwo mwamsanga nthawi yomweyo; ndi kukamuyika mmodzi mu nyumba imodzi, mmodzi mu imzake, ndi mmodzi mu imzake, kuti iwo akakhone kukupatsani inu malangizo, inu amene muti mukafunefune dalitso lalikululu ili limene ife tikulikamba, ubatizo wa Mzimu Woyera.

<sup>3</sup> Usiku watha ife tinali kuyankhula, “chimene Iwo unali.” *Mzimu Woyera Unali Chiyani?* Ndipo ife tinawupeza Iwo kukhala uli basi pafupifupi chirichonse, chimene Mulungu analonjeza kwa ife. U-nhu. Mwa Iwo ife tinapeza basi chimene Mpingo wa Mulungu ukanati usowe. Ife tinawupeza Iwo kuti uli chisindikizo, Mtonthozi, mpumulo, ndi chisangalalo, ndi mtendere, ndi chiwukitsiro. Ndipo zonse zimene Mulungu analonjeza kwa Mpingo Wake, zagona mkati mwa Mzimu Woyera.

<sup>4</sup> Ndipo tsopano, usikuuno, ife tikufuna kulalikira pa, kapena kuyankhulapo, kuphunzitsapo . . . Ine ndiri nayo pafupi

mikwamba itatu kapena inayi ya nkhani pano, kapena Malemba, pa Iwo, mmene. . . Usiku watha ine ndinasiya Konkodanse yanga ya Cruden ili pano, ndipo ine sindinayitenge iyo. Ndipo ine ndimangodutsa chabe mwakukhoza komwe ine ndikanakhoza lero ndi Malemba. Tsopano, ndipo mawa. . . Usikuuno ife tikuphunzitsa pa: *Kodi Chanji Cholinga Chotani Kuti Mulungu Atumize Mzimu Woyera?* Kodi Iwo ndi wa chiyani? Ngati Iwo uli chinthu chachikulu chotero, ndiye nchifukwa chiyani Mulungu anawutumiza Iwo?

<sup>5</sup> Ndiye, mawa usiku ife tikufuna kuti tidzayankhule pa: *Kodi Iwo ndi wa Inu?* ndi *Kodi Iwe Umawulandira Chotani Iwo?* ndi *Kodi Iwe Umadziwa Bwanji Pamene Iwe Uli Nawo Iwo?*

Ndiyeno, ife tikatha kudutsa mu zimenezo, ndi Malemba, kuzifotokoza izo mwa Malemba, pogwiritsa ntchito Malemba kwa zinthu zonse, ndiye iwo amene akufunafuna Mzimu Woyera adzabwera kutsogolo pamenepo. Ndiyeno ine ndikuyembekeza chitsitsimutso chiyambika, kuchokera pamenepo mpakana, kuti tizisunthira patsogolo ndiye ndi Mzimu Woyera.

<sup>6</sup> Tsopano, pokhala kuti mawa usiku ambiri akhoza kukhala kanthawi pang’ono mu zipinda mu mpingo, ine ndikumverera kuti ngati ife tikanati titenge atumiki ochuluka ndi anthu awo omwe ali nako kudziwa mu kuwatsogolera anthu kuti alandire Mzimu Woyera, kuti awalimbikitse iwo, kuti apite mu nyumba ndi—mayi ndi mwamuna wake, kapena—kapena ndi winawake yemwe akufuna Mzimu Woyera, yemwe ali wolangizidwa bwino pa choti achite.

Ngati inu mutati mungopereka foni nambala yanu kapena adiresi kwa abusa, usikuuno kapena mawa usiku. Mungopereka iyo kwa M’bale Neville, ndiye izo zitisungira ife kusunkhana mwa msonkhano. Mungopereka foni nambala yanu kumene ife tingakhaze kukufikirani inu. Ndiyeno kuti, “Ine ndidzakhlapo, ndipo ngati ife. . . inu mukufuna kundiyika ine mu nyumba.” Ngati ndizo—mkazi yekha, ndiye ife tikhoza kutumiza mkazi, mwaona, kwa mkazi uyu. Ndiyeno, ngati ndi mu nyumba mmene muli mwamuna ndi mkazi wake, bwanji, ife tikhoza kutumiza mtumiki.

Ndipo ife tidzakhala okondwa kuti tikhale nanu inu kuti tigwirizane, chifukwa ine ndikudziwa inu muli, mmodzi aliyense, okondweretsedwa mu izi, zofunika kwambiri izi. Ndipo kumbukirani, “Iye amene apulumutsa moyo kuchokera ku kulakwitsa kwake, waphimba unyinjira wa tchimo.” Mwaona? Ndipo Mkwatibwi wa Khristu akuchita njala ndi ludzu. Iye ali mu kumva kupweteka, kuti apereke kubala kwa ana a Mulungu.

<sup>7</sup> Ndipo tsopano, usikuuno, ife tisanati tiwerenge Malemba, tiyeni ife tiweramitse mitu yathu mphindi chabe kwa pemphero. Ndipo basi ife tisanapemphere, inu ndi mitu yanu yoweramitsidwa, kodi inu mungakhale ndi

chopempha? Ingokwezani manja anu ndi kuti, “Mulungu, ine mwakachetechete ndikukweza manja anga. Ine ndiri nacho chosowa. Ine ndikupemphera kuti Inu mundithandize ine, O Ambuye.” Mulungu adalitse aliyense wa inu. Iye akuwona manja anu. Angelo alemba zopempha zawo.

<sup>8</sup> Ndipo, Atate Akumwamba, ife tsopano tikubwera, kukuyandikirani Inu kachiwiri mwa pemphero. Chimene, mosakaika kuti pemphero lapangidwa kale pakati pa ana a Mulungu usikuuno, mu malo aang’ono ano, ndipo kuti nyimbo zayimbidwa kale, ndipo ife takwezera mitima mwa zisangalalo zachimwemwe pa matamando a Mulungu.

<sup>9</sup> Davide anati iye akanati abwere mu msonkhano wa oyera ndi kupanga zopempha zake kudziwika. Ndipo usikuuno, pakhala pali manja ambiri. Mwinamwake, mwina, ine ndikanati, magawo makumi asanu ndi atatu pa zana a iwo omwe akhala mu nyumba yino usikuuno akweza manja awo popereka zopempha. Zikusonyeza, Ambuye, kuti ife sitingakhoze kumangopita wopanda Inu. Ife tiyenera kukhala ndi Inu, tsiku ndi tsiku. Inu ndinu Moyo wathu, chisangalalo chathu, thanzi lathu, nyonga zathu zolimbikitsa, chikhazikitso chathu, chomangira chathu, chishango chathu kwa mdani.

Ndipo ife sitikanakhoza basi kumenya nkondo iyi ya moyo popanda Inu. Izo zikanakhoza kukhala zosatheka kwathunthu kwa ife kuti tichite izo, ndipo ife tiyenera mwathunthu kudalira pa Inu. Chifukwa, ife tikudziwa kuti ife tikuyenda kupyola mu dziko la mdima lachimbuuzi. Pa mbali iliyonse mdani watifooketsa ife, pa kutipatsa misampha ndi makhwekhwe. Njira zathu, Ambuye, zadzaza ndi misampha ya mdani, kuti zitisokoneze ife.

<sup>10</sup> Ndipo ife, nafenso, tikudziwa, pakutha pa ulendo ife tiri ndi khwawa lalitali lija, lamithunzi lotchedwa imfa kuti tiyende kudutsamo. O Ambuye, ndani ati adzatigwire manja athu ndiye? Ife tikufuna kuti tikudziweni Inu tsopano, Ambuye. Ife tikufuna tidziwe kuti Inu mwagwira manja athu, ndipo ife tagwira dzanja Lanu, kuti ife tikhoza kukhala nacho chitsimikizo chozikika icho kuti pamene ife tifika ku mphindi yayikulu yotsiriza iyo ya moyo wathu, imene polowa mu khomo ilo lotchedwa imfa, kuti ife tingakhoze kunena ndi woyera wakale, “Ine ndikumudziwa Iye mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake, ndipo ine ndikudziwa kuti pamene Iye ayitana, ine ndidzatuluka kuchokera pakati pa akufa.”

<sup>11</sup> Tsopano, Atate Mulungu, ife tikanati tipemphere kuti Inu mudalitse zopempha zathu ndi kusonkhana kwathu. Dalitsani Mawu Anu. Ndipo ngati ine ndingati ndinene chirichonse chimene chikanakhala chosiyana ndi Mawu Anu kapena chifuniro Chanu, Inu mukadali nayobe mphamvu kuti mutseke kamwa, monga Inu munachitira mu khola la mikango pamene

Daniele analimo. Ndipo ife tikupemphera, Ambuye, kuti Inu mutsegule makutu ndi mitima usikuuno, kuti, ndi kulenga mwa iwo njala ndi ludzu. Mulole iwo akakhale aludzu mwakuti iwo sangakhoze kugona kapena kupuma, paliponsepo, kufikira Mtonthozi atabwera.

<sup>12</sup> Ife tikukhulupirira kuti ife tikukhala mu masiku otsiriza, mu mthunzi wa Kudza Kwake. Ndipo ndiko kumene Mauthenga awa akulunjikidwira, Ambuye. Ndi kuti anthu asalalire, atenge chenjezo. Ndipo mulole, usikuuno, ife tingovula chigoba, pakali pano, kuchiyika icho pa mbali ya benchi, kuti, “Ambuye Mulungu, ine ndine wolandira kwa Inu. Lolani Mzimu Wanu uyenderere kudutsa mwa ine. Ndiwumbeni ine ndi kundipanga ine monga mwa chifuniro Chanu. Ine ndikupereka mtima wanga, mphamvu yanga, zonse zanga, ku cholinga Chanu.”

<sup>13</sup> Timvereni ife, Ambuye. Ife sitiri pano kuti tiwonedwe, pa usiku wamvula uno. Ife sitiri pano basi chifukwa chosowa malo ena oti tipiteko. Ife tiri pano chifukwa cha cholinga chimodzi cha kachetechete, chopatulika, choyera mu mitima yathu, ndicho kuti, tiyandikire pafupi kwa Inu, pozindikira kuti Inu mwalonjeza kuti ngati ife titi tiyandikire pafupi kwa Inu, Inu mukanayandikira pafupi kwa ife. Ndipo ndicho chifukwa ife tiri pano. Iye amene abwera mkati wanjala sapita kunja wanjala. “Odala ali iwo amene amva njala ndi ludzu chifukwa cha chilungamo,” anatero Yesu, “pakuti iwo adzachita kukhutitsidwa.” Ndipo ngati ife titi tipemphe mkate, ife sitilandira mwala. Ife tiri nacho chitsimikizo chimenecho. Ndipo ngati ife titi tipemphe nsomba, ife sitilandira njoka. Koma, Mulungu Atate wathu atidyetsa ife ndi Mana Akumwamba, Mawu Ake ndi Mzimu Wake zimene zikuchitira umboni wa Iye. Yankhani mapemphero athu, Ambuye, ndi zopempha zathu, pamene ife mopitirira tikuyembekezera pa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupemphera. Amen.

<sup>14</sup> Tsopano, inu amene mukusunga Malemba awa, ngati inu mungati mutembenuze ndi ine ku Yohane Woyera kachiwiri, mutu wa 14. Ife tikufuna kuti tiyambire pa mutu 14 wa Yohane Woyera. Ndipo tiyeni tiyambire cha pa ndime ya 14, Yohane Woyera 14:14, ndipo tingowerenga gawo la Lemba ili. Tsopano, mu izi inu mupeza zochuluka za nkhani imene ine ndikufuna kuti ndiyankhulepo usikuuno.

<sup>15</sup> Ndipo kumbukirani, inu amene muli nawo Mabaibulo a zolemba zofiira, izo ziri mu zofiira, izi ziri. Ndi Mawu omwe Yesu Mwiniwake anawayankhula, koterono ife tikhoza kukhala nacho chitsimikizo kuti izo zidzakhala basi monga Iye wanenera. “Kumwamba ndi dziko zidzapita, koma Mawu Ake sadzalephera konse.”

Tsopano ife tati tiwerenge kuchokera ku ndime 14 ya mutu wa 14.

*Ngati inu muti mudzapemphe chirichonse mu dzina langa, ine ndidzachichita icho.*

Ndi lonjezo lodala bwanji!

*Ngati inu mundikonda ine, sungani malamulo anga.*

*Ndipo ine ndidzawapempha Atate, ndipo iye adzakupatsani inu Mtonthozi wina, kuti akhoze kumakhala ndi inu kosatha;*

*Ngakhale Mzimu wa choonadi; amene dziko silingakhoze kuwulandira, chifukwa ilo silimuwona iye, . . .*

Tsopano, inu amene mukanakhala mukuwerenga kuchokera mu Baibulo la Chigriki, mukanakhoza kuziwona izo umu, osatha. . . *Kumuona* pamenepo zikutanthauza “kumvetsa.” “Pakuti dziko silimumvetsa Iye ayi.” Izo ndi zoonza kwambiri. Ndiroleni ine ndiwerengenso izo tsopano.

*Ngakhale Mzimu wa choonadi; umene. . . choonadi; amene dziko silingathe kumulandira, chifukwa ilo silimuwona iye, ngakhale kumudziwa iye: koma inu mukumudziwa iye (ndani? Mtonthozi); pakuti iye akukhala ndi inu pakali pano (tensi yatsopano), . . . iye akukhala ndi inu, ndipo adzakhala ali mwa inu.*

Kodi Iwo ndi chiyani? Mtonthozi yemweyo.

*Ine sindidzakusiyani inu opanda chitonthozo: Ine . . .*

Aliyense akudziwa kuti “Ine” ndi puronauni ya umwini.

*. . . Ine ndidzadza kwa inu.*

*Komabe kanthawi pang’ono, ndipo dziko silidzandiwonanso ine; koma inu mudza. . . koma inu mudiwona ine: chifukwa ine ndiri moyo, inu mudzakhhalanso moyo.*

*Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate anga, ndi inu mwa ine, ndi Ine mwa inu.*

Pamenepo pakhala pa chirikati pa lingaliro langa, koma ife tiwerenga mopitiriza pang’ono. Ndiroleni ine ndiwerengenso izo tsopano, kachiwiri.

*Pa tsiku limenelo (tsiku lalikululu, tsiku lachiweruzo), tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, ndi inu mwa ine, ndi Ine mwa inu.*

*Iye yemwe ali nalo lamulo langa, ndi kuwasunga iwo, iye ndi yemwe amandikonda ine: ndipo iye yemwe andikonda ine adzakonedwa ndi Atate anga, ndipo ine ndidzamukonda iye, ndipo ndidzadziwonetsera inemwini kwa iye.*

*Yudasi anati kwa iye, osati Iskarioti, Ambuye, izo ziri motani kuti inu mudzadziwonetsera nokha kwa ife, ndipo osati kwa dziko?*

Ndilo, *kosmos*, “dongosolo la dziko.” Ngati inu muli ndi kuwerenga kwa mmalire pamenepo, inu muzindikira. Langa pali “g,” ndipo ilo likunena cha apa, “*kosmos*, kapena zochitika za mdziko.” Ndiyo mipingo, ndi zina zotero, mwaona.

*. . . izo ziri motani kuti inu mudzadziwonetsera nokha kwa ife, ndipo osati kwa iwo? Inu mungakhoze kuchita izo motani?*

*Yesu anayankha ndipo anati kwa iye, Ngati munthu andikonda ine, iye adzasunga mawu anga: (ameni) ndipo Atate anga adzamukonda ine, ndipo ife tidzabwera kwa iye, ndi kudzamupanga pokhala pathu ndi iye.*

*Iye amene sandikonda ine sasunga maneno anga: . . .*

Akhoza kusunga zonena za mpingo; koma kusunga zonena Zake, inu mukuona.

*. . . ndipo mawu amene inu mukuwamvawa si anga, koma Atate omwe anandituma ine.*

*Zinthu izi ine ndayankhula kwa inu, pokhala ndikanalipobe ndi inu.*

*Koma Mtonthozi, yemwe ali Mzimu Woyera, yemwe Atate ati adzatumize mu dzina langa, iye adzakuphunzitsani inu zinthu zonse, ndi kubweretsa zinthu zonse izi (ndiwo, Mawu Ake) ku kukumbukira kwanu, chirichonse chimene ine ndanena kwa inu.*

Kodi ndi cholinga chanji chimene Mulungu anatumizira Mzimu Woyera ndiye? Mulole Iye awonjezere madalitso Ake ku Mawu Ake.

<sup>16</sup> Yesu ananena, kuti, “Pa tsiku limenelo inu mudzadzidwa kuti ine ndiri mwa Atate, ndipo Atate ali mwa Ine; ndipo inu muli. . . Ine ndiri mwa inu, ndipo inu muli mwa Ine.” Tsopano, ngati ife timati tinene izi. . .

<sup>17</sup> Tsopano, kumbukirani, izi zikhala ziri pa tepi.

Munthu wamalonda wa Chikhristu, wochokera ku Louisville, anandiyimbira ine kanthawi kapitako. Ndipo iye anati, “Ndi chamanyazi, Billy, kuti Mauthenga awa, monga inu munanenera usiku watha, samafika kwa zikwi makumi anai kuno mmalo mwa zana ndi makumi asanu, kapena mazana awiri, anthu mazana atatu ku kachisi wanu wamng’ono.”

<sup>18</sup> Ine ndinati, “Bwana, mu miyezi isanu ndi umodzi kuchokera pano, ngati Yesu akachedwa, kuzungulira dziko lonse adzamva izi.” Mwaona?

Matepi amenewo amapita konsekonse pa dziko, mwaona, konse kuzungulira. Ndipo, chotero, ife tiri kuphunzitsa pano tsopano basi zimene ife timakhulupirira kuti ziri Choonadi, ndi chimene ife tachipeza kuti Mulungu watsimikizira icho kwa ife kuti chiri Choonadi.

<sup>19</sup> Tsopano, cholinga, chinali chiyani—cholinga cha Mulungu chinali chiyani pa kutumiza Mzimu Woyera? Tsopano, ine ndikanati ndizilembe zimenezo apo, Yohane 14, kuyambira pa ndime ya 14, ndi kuwerenga kudutsa mu mutuwo, mwa maziko. Cholinga cha Mulungu, ife tikupeza apa, mu kutumiza Mzimu Woyera, chinali cholinga chimodzi, kuti Mulungu iyemwini akhoze kumakhala mu Mpingo Wake ndi kupitiriza madongosolo Ake kupyolera mu Mpingo. Kutu, Mulungu anali mwa Khristu, akupitiriza madongosolo Ake kupyolera mwa Khristu; kuchokera kwa Khristu, kupita mu Mpingo, kupitiriza ntchito Yake kupyolera mu Mpingo.

<sup>20</sup> Tsopano, ife tikudziwa chimene Mzimu Woyera uli. Ife tinapeza, usiku watha, kuti Ndiwo Mulungu.

Tsopano, pamene ife tiganiza za Mulungu, Atate, monga Yesu anamukamba pano, Atate Ake; Mulungu, Mwana, monga Yesu; Mulungu, Mzimu Woyera, monga chomwe ife tikuwutcha Iwo lero. Tsopano, izo sizikutanthauza kuti pali atatu apawokha, Amulungu osiyana. Izo zikutanthauza kuti pali Mulungu mmodzi mu maudindo atatu.

Mulole ife tinene izo monga chonchi. Zonse zimene Mulungu anali, Iye anazitsanulira mwa Khristu, chifukwa Iye anadzikhuthula Iyeyekha ndipo anazitsanulira Izo mwa Khristu. “Ndipo Khristu anali chidzalo cha Umulungu mu thupi.” Zonse zimene Yehova anali, Iye anazitsanulira izo mwa Khristu.

Ndipo zonse zomwe Khristu anali, Iye anazitsanulira mu Mpingo; osati mwa munthu mmodzi, koma mu Thupi lonselo. Pamene, pomwe ife tibwera limodzi mu umodzi, ife tiri ndi Mphamvu. Zonse zimene Mulungu anali, zinali mwa Khristu; ndi zonse zimene Khristu anali, ziri mwa inu.

“Pakuti Mulungu anapangidwa kukhala thupi, ndipo anakhala pakati pathu.” Timoteo Woyamba 3:16, ngati inu mukuzilemba izo, “Popanda kutsutsana chinsinsi cha umulungu ndi chachikulu: pakuti Mulungu anawonekera mu thupi, ndipo ife tinamugwira Iye. Mulungu, Yehova, anapangidwa kukhala thupi, ndipo ankayenda pa dziko lapansi, ndipo ife tinamuwona Iye ndi maso athu.”

<sup>21</sup> Inu mukudziwa, mu mutu womwewo, wa Yohane 14, Filipo anati, “Ambuye, tiwonetseni ife Atate, ndipo icho chitikwanira ife.”

<sup>22</sup> Yesu anati, “Ine ndakhala ndiri ndi iwe motalika chotere, Filipo, ndipo iwe sukundidziwa Ine? Pamene iwe wandiwona Ine, iwe wawaona Atate. Ndipo iwe unena bwanji kwa Ine,

“Tiwonetsereni ife Atate?” Mulungu anapangidwa kukhala thupi.

<sup>23</sup> Tsopano ndi izi apa. Atate anali Mulungu pamwamba pa inu, ife timati. Ife takhala tiri kuyambira pa Adamu. Mulungu, Atate, anali pamwamba pa Mose ndi ana a Israeli, mu Lawi la Moto. Kenako, Mulungu nafe, mwa Khristu; anayenda ndi ife, anayankhula ndi ife, anadya ndi ife, anagona ndi ife. Mulungu pamwamba pa ife; Mulungu nafe; ndipo tsopano Mulungu mwa ife. Zonse zimene Mulungu anali, zinabwera mwa Khristu; zonse zimene Khristu anali, zinabwera mu Mpingo.

Ndi chiyani icho? Mulungu akugwira ntchito mwa inu. Kulikonse mu dziko kumene Iye angafune kuyitana pa inu, inu muli komweko, kugwira ntchito mwa inu kuti achite chifuniro Chake chabwino. Momwe ife tiyenera kumuthokozera Mulungu chifukwa cha zimenezo! Mulungu, Mzimu Woyera, watumizidwira pa cholinga chakuti Mulungu azikhala mu Mpingo Wake, akuyenda kupyolera mu m’badwo uliwonse, akuchita chifuniro Chake Chaumulungu.

<sup>24</sup> Pamene anthu akusekani inu, iwo sali kukusekani inu, iwo akumuseka Iye yemwe anakutumani inu. Kotero Yesu anati, “Odala muli inu pamene anthu ati adzanene choyipa cha mtundu uliwonse motsutsa inu, mwabodza, chifukwa cha Dzina Langa. Odala muli inu.” Ndipo, kachiwiri, “Onse amene akhala moyo mwaumulungu mwa Khristu Yesu adzasautsika ndi kuzunzidwa.”

Pakuti, pamene Mulungu anadzipangitsa Iyeyekha kudziwika mwa Khristu, iwo anamuda Iye. Ndani anamuda Iye, moyipisitsa? Mpingo. Mpingo unamuda Iye, moyipisitsa. Iwo ankamuda Iye moyipitsitsa kuposa—zidakhwa. Iwo anamuda Iye moyipitsitsa kuposa anthu ena onse. Iwo unali mpingo umene unkamuda Iye. Kotero, chotero, pamene inu muwona *kosmos*, “Dongosolo la mdziko, dziko silinamudziwe Iye ayi,” zikutanthauza “mpingo,” wotchedwawo, “sunamuzindikire Iye ayi. Iye anadza kwa Ake omwe, ndipo Ake omwe sanamulandire Iye ayi.”

“Koma onse amene anamulandira Iye, kwa iwo Iye anawapatsa mphamvu kuti akhale ana aamuna a Mulungu, kwa iwo omwe anakhulupirira pa Dzina Lake.” O, momwe ife tiyenera tizimukonda Iye ndi kumupembedza Iye! Cholinga cha Mulungu, kufuna kuti akhale mu chiyanjano!

<sup>25</sup> Monga, ife tisanausiye mutu uwu, tiyeni tigwiritse ntchito izi; mu masiku a Rute, mu lamulo la chiwombolo, pamene Naomi anali atachoka ku dzikolo, chifukwa cha yesero, nthawi ya zovuta. Iye anapita mu dziko la Amoabu, limene linali lofunda chabe, Akhristu mwadzina chabe. Chifukwa, Amoabu anachokera kwa mwana wamkazi wa Loti, ndipo iwo anali ongotchedwa okhulupirira, ndi osakanizika. Ndiyeno mwamuna



wake anafa, ndi ana ake amuna anamwalira. Ndipo ali pa ulendo wa kwawo, Naomi. . . Rute ndi Naomi, ali pa ulendo wake wopita kwawo, iye. . . Mmodzi wa apongozi ake aakazi Oripa, iye anati kuti iye akanabwerera ku dziko la kwawo, ku milungu yake, ndi ku mpingo wake, ndi kwa anthu ake. Ndipo Naomi anayesa kuti amufikitse Rute kuti abwerere, koma iye anati, “Anthu ako ali anthu anga. Mulungu wako ali Mulungu wanga. Kumene iwe ukafere, kumeneko ine ndikafera. Kumene iwe ukayikidwe, kumeneko ine ndikayikidwa. Ndipo ine sindidzabwerera mmbuyo ayi.”

<sup>26</sup> Ndi pamene munthu wagwira masomphenya. Sizinapange kusiyana kulikonse chimene anthu ake ananena, “Iwe ukupita kumeneko kuti ukakhale woyera-wodzigudubuza kapena chinachake.” Zimenezo sizinapange kusiyana kulikonse kwa Rute. Pamenepo panali cholinga cha Mulungu choti chikwaniritsidwe.

<sup>27</sup> Ndipo basi motsimikiza monga inu mukumvera njala usikuuno kufuna Mzimu Woyera, ndi chinachake mwa inu, chikukukokani inu, kuti cholinga cha Mulungu mu moyo wanu chiyenera kuti chikwaniritsidwe, basi monga izo zinali ndi Rute.

<sup>28</sup> Nkhaniyo ndi yokongola kwambiri! Ine sindingakhoze basi kuyisiya iyo, kwa mphindi. Inu mukudziwa lamulo la chiwombolo, kuti pamene Boazi. . . Inu mukuyidziwa nkhaniyo ya momwe Rute anakunkhira mu munda ndipo anapeza kukonedwa ndi Boazi. Ndipo iye asanamukwatire iye, iye ankayenera kuti awombole zonse zimene Naomi anali atataya. Ndipo mmodzi yekha yemwe akanakhoza kuwombola munda wotayika wa Naomi, mu lamulo la chiwombolo, anali wachibale wapafupi; ankayenera kuti akhale munthu wachibale asanati iye awombole. Ndipo ameneyo anali munthu wachibale wake wapafupi kwambiri. Ndipo iye ankayenera kuti apange chisonyezo cha pagulu, kunjwa kwa chipata, kapena kuvomereza kwa pagulu kuti iye anali atawombola zonse zimene Naomi anali atataya. Ndipo Boazi anachita izo pa kuvula nsapato yake pamaso pa aakulu, ndipo anati, “Ngati alipo munthu aliyense pano yemwe ali nacho chirichonse chimene chiri cha Naomi, ine tsiku lino ndachiwombola icho.”

<sup>29</sup> Ndipo ndimo momwe Mulungu anachitira, anatsatira malamulo Ake Omwe. Mulungu sangakhoze kutsatira, kukupatsani inu lamulo limodzi kuti mulitsatire ndipo Iye nkumatsatira lina. Iye amatsatira malamulo Ake Omwe. Ndiye, Mulungu, pofuna kuti awombole mpingo wotayika, dziko lotayika, chirengedwe chotayika; Mulungu, Yemwe ali wopanda malire mu Mzimu, kuti awombole mtundu wa anthu wotayika, Mulungu Mwiniwake anadzakhala wachibale, Munthu, Mwana yemwe Iye anamulenga mu chibelekero cha Maria. Ndiyeno Iye anapanga chisonyezo, kapena umboni; kunjwa kwa zipata za Yerusalemu, Iye anatumukidwira mmwamba

pakati pa mmwamba ndi dziko lapansi, ndipo anafa, ndipo anawombola chirichonse. Ndipo mu kuwukha magazi, Iye anawuyeretisa Mpingo kuti Iye Mwiniwake akakhoze kumakhala mmenemo, ndi kuyanjana ndi kuyankhulana nawo, malo otayika a chiyanjano aja kuchokera ku munda wa Edeni kumene Mulungu ankabwera pansu usiku uliwonse, nthawi ya mpingo.

Kodi inu munazindikira, Mulungu amabwera pansu mu kachisisira ka tsiku, mkulowa kwa dzuwa. Pali chinachake chokhudza pamene kuyamba kuti kukhale usiku, anthu amaganiza za mpingo ndi za Mulungu; Akhristu. Inu mumawona dzuwa likulowa, inu mumazindikira kuti dzuwa lanu likulowa.

<sup>30</sup> Ndipo mu chisisira cha usiku Iye amakhoza kubwera pansu ndi kuyankhulana nawo iwo. Ndipo pamene Iye anataya chiyanjano chimenecho, chifukwa tchimo silikadamulola Iye kuchita izo.

Ndiyeno Iye anapangidwa thupi ndipo anakhala pakati pathu, polinga kuti Iye akanakhoza kubwereranso kachiwiri kwa munthu, ndi kumakhala mwa munthu, ndi kumubwezeretsa munthu ku chikhalidwe cha chiyanjano ndi Iye kachiwiri, ndi kumupatsanso iye ufulu wopatsidwa ndi Mulungu. Ndicho chimene Iye anachita.

<sup>31</sup> Ndicho cholinga cha Mzimu Woyera. Ndiwo Atate, kachiwiri, Mulungu Atate kukhala mwa inu, kuchita zolinga Zake, kuti atsirize dongosolo Lake la chiwombolo; kugwira ntchito kupyolera mwa inu, kukupangani inu wogwira ntchito ndi Iye; kukupatsani inu malo, kukupatsani inu gawo chifukwa cha m'bale wanu wakugwa, ndi mlongo wotayika; kukupatsani inu Mzimu Wake ndi chikondi Chake, kuti mupite mukasake wotayika, monga Iye anachitira mu munda wa Edeni. “Adamu, Adamu, uli kuti iwe?” Ndicho chimene Mzimu Woyera umachita kwa mwamuna kapena mkazi. Pamene Iwo ukhudza mu mtima mwawo ndi kutenga pokhala Pake, pali ludzu ndi njala yofuna miyoyo yotayika.

Ndilo lomwe liri vuto ndi misonkhano lero. Mulibe kukhudza kokwanira kwa Mzimu mmenemo, kukafunafuna miyoyo ya otayika ndi omwe akufa. Zachuluka ndi za kupanga dzina, kapena mpingo, kapena nyumba, kapena chipembedzo, mmalo mwa dongosolo lopindula-miyoyo. Ndi zachisoni bwanji! Ife tikanakhoza kungokhala pa izo mochuluka.

Mulungu anadzitsanulira Iyemwini mwa Khristu. Kulondola.

<sup>32</sup> Khristu anadzitsanulira Iyeyekha mwa Mpingo. Chotero, tsopano penyani, “Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, ndipo inu muli mwa Ine, ndipo Ine ndiri mwa inu. Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa izo.” Pakuti, ndi, chinthu chonsecho chiri dongosolo limodzi la chiwombolo likubwera pansu, Mulungu ameneyo akubwereranso kuti adzakhale mkati,

ndi kukhala nawo, ndi kuyankhula kwa anthu Ake, monga Iye ankachitira pachiyambi.

Tsopano, ndiye, mwamsanga pamene Iye ati awutengere Mpingo Wake mu zikhalidwe zoyankhulana, kuwutengera Mpingo Wake ku malo amene Iye angakhoze kuyenderera Iyeyekha modutsamo, ndi kuwukonda, ndi kuwukakamiza, ndi kuyanjana, ndiye pamenepo padzabwera Edeni. Iye adzawutengera Mpingo Wake kubwerera kumene Iwo—Iwo unamusiyira Iye, kubwerera ku Edeni kachiwiri, uko kumene Iwo unagwera. Iwo, tsopano... Ndi kumene Iwo unapanga kuyamba Kwake koyamba, kapena kugwa. Uko ndi kumene Iwo uti udzatengedwere kubwerera kumene, ndi cholembapo choyera chirichonse cha chiwombolo, kuwabwezera iwo molunjika mmbuyo ku malo amenewo kachiwiri.

<sup>33</sup> Mpingo wakhala uli mu dziko kwa nthawi yina. Ndipo Mpingo, mwenimweni, kutachitika kukonzanso, kwa zaka mazana khumi ndi asanu za mibadwo ya mdima... Lutera anali wokonzanso woyamba kuti abwerepo kutatha kubwera kwa atomwi. Ndiyeno pamene Lutera anabwerapo, Mulungu anapendeketsa pang'ono pokha za Mzimu ndipo anawutsanulira Iwo pa Mpingo, mu kulungamitsidwa. Ndiyeno mu masiku a Wesile, Iye anatsanulira pang'ono penanso za Iyemwini, kupita mu kuyeretsedwa. Ndipo monga m'badwo wakula mopitirira, kufika ku nthawi yotsiriza, Mulungu wakhala akuwudzazitsa Mpingo Wake. Tangoyang'anani kozungulira ndipo mupeze ngati ndizo Zoon, kapena ayi.

<sup>34</sup> Tayang'anani pa m'badwo wa Lutera, inu amene mumawerenga mbiri yakale, tayang'anani pa chitsitsimutso chawo ndi chimene iwo anachita. Taonani kukulirapo kumene chitsitsimutso cha Wesile chinali, ndi kuchuluka kwa mphamvu zina zochulukuka zimene iwo anali nazo, koma mwa ochepa. Penyani mu masiku a Pentekoste, chitsitsimutso chimene iwo anali nacho pamenepo, ndi kusesa, kotambalala bwanji.

<sup>35</sup> Komanso, *Mlendo Wathu wa Lamlungu*, pepala ya Katolika, inapereka kuvomereza kuti Apentekoste anabala otembenuka milioni imodzi zikwi mazana asanu mu chaka chimodzi, kuchita moposa mipingo inayonse palimodzi. Akatolika anangosintha kokha, amati, milioni. Mu *Mlendo wa Lamlungu* mwawo momwe, pepala yotchedwa *Mlendo wa Lamlungu*, inapereka kunena kwakuti Apentekoste anachita mowaposa iwo.

Ndipo, kumbukirani, kutembenuka kwa Chipentekoste ndi kutembenuka kodzazidwa Mzimu Woyera. Mwa ochepa, poyamba pomwe, pa mbali ya chigwa kunja uko, ali ndi—bangwe wakale. Ndipo akazi sankakhoza kukwanitsa ngakhale peyara ya masitonkeni. Atagona panja ku tinjira ta msewu wa njanji, ndipo akutola chimanga ndi kumachikonola icho, ndi kumakonzero mkate wa ana awo. Koma kodi izo zafika kuti?

Mpingo woyima mwamphamvu-kwambiri mu dziko lero, osati mwa maso a dziko, koma mwa maso a Mulungu, chifukwa Iye akutsimikizira izo ndi zimene Iye akuwachitira iwo. Iye akudzitsanulira Iyeyekha mwa iwo, kutsanulira Iwo mkati.

<sup>36</sup> Zindikirani tsopano chimene chinachitika, Mulungu kudzitsanulira Iyemwini mwa iwo. Tsopano Mpingo wafika pa malo, kuchokera kwa Lutera, Wesile, ndipo chitsitsimutso chiri kuchitika pa Apentekoste; ndipo tsopano kupita mu m'badwo uno umene ife tikubweramo tsopano, mwa Mzimu Woyera womwewo, kungoti zochulukira za Iwo. Tsopano, pamene Achilutera aja kumbuyo uko anali atapulumutsidwa, iwo analandira gawo la Mzimu Woyera. Pamene Amethodisti anali atayeretsedwa, imeneyo inali ntchito ya Mzimu Woyera. Mwaona, ilo linali gawo la Mzimu Woyera. "Iwo popanda ife sangapangidwe kukhala angwiro," limatero Lemba. Mwaona?

<sup>37</sup> Tsopano, Mulungu, monga Kuwala kwayamba kuwala mu masiku otsiriza, Iye akuyembekezera ife, chinthu chachikulu kuchokera kwa ife. Chifukwa, "Pamene pali zochuluka zitaperekedwa, pamenepo pali zochuluka zikuyembekezeredwa." Kotero Iye adzafuna zochuluka kwambiri za ife kuposa momwe Iye anachitira ndi Achilutera kapena Achimethodisti, chifukwa ife tikuyenda mu Kuwala kokulirapo, ndi Mphamvu yokulirapo, ndi wokulira... u—umboni wokulirapo kuposa umene iwo anali nawo. Tsopano, ife tiri nawo umboni wokulirapo wa chiwukitsiro. Ife tiri nazo zinthu zolimba mochulukira, zotsimikizika mochulukira kuposa zomwe iwo anali nazo.

<sup>38</sup> Koma izo zangokhala basi monga ine ndinanenera ku koleji ya Chilutera, osati kale litali.

Iwo anati, "Kodi ife tiri ndi chiyani?"

Ine ndinati, "Munthu anabzala munda wa chimanga. Timasamba toyamba tating'ono tinatulukira, ndipo iye anati, 'Zikombo Ambuye chifukwa cha—mbewu ya chimanga!' Mwakuyankhula kwina, iye anali nacho icho, koma iye anali nacho icho kokha mu mawonekedwe oyambirira. Pang'ono ndi pang'ono, icho chinakhala phesi."

Ndipo nyayaye zinatulukira pa icho, chomwe chinali Amethodisti.

<sup>39</sup> Ngati inu mungayang'ane chirengedwe, inu muwona Mulungu akugwira ntchito. Pali chinsinsi chagona mmenemo chimene chimapita ngakhale ndi utumiki wanga. Mwaona? Ichu, poyang'ana chirengedwe, kuwona momwe icho chimachitira, m'badwo wake ndi nthawi yake, iwe ukhoza kuwona kumene iwe ukukhala. Penyani m'badwo.

<sup>40</sup> Tsopano, ndiye, Amethodisti, iwo anali ngayaye. Iwo anayang'ana mmbuyo kwa Achilutera, nati, "Ife tiri nako kuyeretsedwa; inu mulibe kanthu mwa Iwo."

Pang’ono ndi pang’ono, kuchokera ku mkaka umenewo, kuchokera kwa Amethodisti, kunatulukira mbewu ya . . . khutu la chimanga. Imeneyo inali Pentekoste.

Ndi iwo pamenepo, kulungamitsidwa, siteji imodzi ya Iwo. Kuyeretsedwa, siteji yina ya Iwo. Mzimu Woyera, siteji yina ya Iwo; Pentekoste. Lutera, Wesile, Pentekoste.

<sup>41</sup> Tsopano Pentekoste ikuchita chiyani? Ine ndikuyifanizitsa iyo, chifukwa, mu Pentekoste, iyo inabweretsanso, osati tsamba lobiriwira, osati ngayaye, koma . . .

Chimanga sichingakhoze kunena kwa ngayaye, “Ine ndiribe nawe iwe ntchito.” Kapena, ngayaye siyingakhoze kunena kwa—tsamba, “Ine ndiribe nawe ntchito iwe,” chifukwa moyo womwewo umene unali mwa tsamba unapanga ngayaye. Moyo womwewo unali mu ngayaye unapanga khutu.

Ndipo iwo unali mpingo wa Chilutera umene unapanga mpingo wa Chiwesile. Unali mpingo wa Wesile umene unapanga Pentekoste.

Koma, Pentekoste, ndi chiyani iyo? Ndiyo kubwezeretsa kwa mtundu womwewo wa njere imene inapita mu nthaka pa chiyambi, kubweretsanso chidzalo chonse cha Mphamvu ya Pentekoste, mwa ubatizo wa Mzimu Woyera, mwaona, mu masiku otsiriza. O, ndi chinthu chachikulu, kuti uyang’ane, kuti ukhulupirire ndi kuti uyang’anepo.

<sup>42</sup> Tsopano mu m’badwo uno umene ife tiri kukhalamo tsopano, m’badwo uno, iwo wapyola pa Pentekoste.

Pentekoste yadzikhazikitsa yokha polowa mu mabungwe, ndipo yayamba kutengera zochuluka kwambiri za mabungwe, “Ife ndife *ichi* ndipo ndife *icho*.” Ndicho chibadwa basi. Inu basi simungachitire mwina. Ndi chibadwa. Iwo azichita zimenezo. Ndi dongosolo, la iwo kuti azichita zimenezo.

Koma Mpingo wasunthira patsogolo. Iwo wapita mokulira, mwamphamvu zochuluka. Ndiko kubwezeretsa kwa mphatso.

Ndipo anthu ambiri a Chipentekoste sakhulupirira mu machiritso Auzimu, utumiki wa Angelo, ndi mphamvu za Mulungu. Achipentekoste ambiri amawatcha masomphenya awa omwe ine ndimawaona, “mdierekezi.” Mabungwe ambiri sangathe ngakhale kukhala ndi kanthu kochita ndi Iwo, mu Pentekoste. Mwaona, ife tasuntha kudutsa zimenezo. Kungokhala monga Amethodisti anatcha Chipentekoste, “kupenga,” chifukwa choyankhula mu malirime. Kungokhala monga Alutera anatcha Amethodisti, “openga,” chifukwa chofuula. Mwaona?

Koma izo zonse ndizo kubwera kwa Mzimu Woyera, mpaka Mpingo waukulu ukhale utadzazitsidwa, ndi kukhomereredwa modzaza, aleluya, [M’bale Branham akugogoda pa guwa kawiri—Mkonzi.] ndi zimphamvu zazikulu za Mulungu

Wamphamvuzonse. Mpaka, iwo ukhale utafika pa malo amene mpaka ntchito zomwe zimene Yesu anazichita ziziwonetseredwa zokha mu Mpingo momwe tsopano. Ife tiri pafupi, amzanga.

<sup>43</sup> Ndiroleni ine ndiyime apa, kwa miniti chabe, kuti titenge chifukwa chimene Mulungu anawuyikira Mzimu Woyera mu Mpingo, kukupatsani inu choyimira china koteru kuti inu mudziwe. Kubwerera mu Chipangano Chakale, pamene—mwana . . .

Mwamuna ankadzipangira iyeyekha nyumba. Iye akapeza mkwatibwi wake, ndicho chinthu choyamba.

Ndiye iye amakhala munthu wamkulu, monga bungwe. Izo zinali zabwino.

Chinthu chotsatira chinali kuchitika, uko kumabwera kubadwa mu nyumba mmenemo. Ndipo pamene Mzimu Woyera, onani, mzimu wina unabwera mmenemo, umene unali mwana wamwamuna. Mwana wamwamuna ameneyo, iye sanali mu ulumuliro wathunthu, ngakhalenso iye sanali wolamulira kufikira iye atafika pa usinkhu wina. Ndipo iye ankayenera kuti atsimikizidwe, choyamba. Inde.

Ndiyeno iwo anali nalo lamulo la kulandiridwa. Kwa inu atumiki, “kukhazikitsidwa kwa mwana wamwamuna,” ndi chimene ine ndikuchikamba tsopano, mwaona, ndiye pamene iye afika pa malo pomwe iye anali kulandiridwa. Yesu anapereka kuwonetsera kokongola kwa izo, pa Phiri la Chiwalitsiro.

<sup>44</sup> Monga ine ndinanena, Mulungu sadzapita konse kunjika kwa malamulo Ake kuti achite chirichonse.

Ngati inu muli ndi chitsime cha kasupe pa phiri *ili*, chikupemerera madzi ponseponse mu mpweya. Ndipo pa phiri lina ili cha *apa*, inu muli ndi mbewu ziri kuwawuka. Inu mukhoza kuyima pa phiri ili ndi kufuula, “O, madzi, thamangira kuno ndi kudzadzazitsa mbewu zanga! O, madzi, fika ku mbewu zanga!” Iwo sadzachita konse zimenezo. Koma ngati iwe utati uchite molingana ndi malamulo okokera pansu, iwe ukhoza kutsirira mbewu zimenezo.

<sup>45</sup> Inu mutakhala ndi munthu wodwala atakhala apa, kapena wochimwa atakhala apa, kapena munthu yemwe akufuna kuti akhale wabwino, sakukhoza kusiya kumwa, sakukhoza kusiya kusuta, sakukhoza kusiya kukhumbira ndi zinthu. Ngati inu mutati mungogwira ntchito molingana ndi malamulo a Mulungu, kulola Mzimu Woyera kubwera mmenemo, ndiye iye salinso mwini wake. Iye, iye adzasiyitsa chinthu chimenecho, chifukwa Mzimu Woyera umamudutsitsa iye. Koma inu muyenera kugwira ntchito molingana ndi malamulo a Mulungu, ndondomeko za Mulungu.

<sup>46</sup> Tsopano, mu Chipangano Chakale, pamene mwana uyu anali atabadwa, iwo ankamuyang'ana iye, kuti awone momwe iye anali kukhalira, khalidwe.

Ndiye atate, pokhala munthu wamalonda wamkulu pa nthawi iyi, mwinamwake mu makumi anai ake kapena makumi asanu, iye sanali kukhala ndi nthawi yoti azimuphunzitsa mwana ameneyu, iyeyekha, kotero iye amapeza. . . Mu masiku amenewo iwo analibe masukulu a aliyense monga iwo ali nawo tsopano, kotero iwo ankapeza yemwe iwo ankamutcha “mlangizi,” kapena “muleli,” mphunzitsi wa sukulu. Ndipo mphunzitsi wa sukulu uyu anali wopambana yemwe iye akanakhoza kumupeza, kuti iye akhale ali woona ndi kumamuuza tateyo zoonza za iye.

<sup>47</sup> Ndiyeno pamene mnyamata uyu amafika pa usinkhu winawake, titi, iye anali atakula. Ngati mnyamata ameneyo anali chigawenga chabe, osati wabwino, wosasamalira ntchito ya bambo ake; chonse chimene iye amaganizira chinali kudzifunitsa ndi kuyenda ndi akazi, kapena—kapena kumwa, kapena kuchita njuga; mjaha wa kavalo; mnyamata ameneyo akanati akhalebe ali mwana wake nthawizonse, koma iye sanali kuyikidwa konse mu malo kuti azilamulira zonse zimene bambo ake anali nazo.

Koma ngati iye anali mnyamata wabwino, ndipo iye anali pa ntchito ya atate ake, ndipo iye anatsimikizira kuti ali mwana woyenera, ndiye iwo amakhala ndi mwambo. Iwo amamutengera mnyamatayo kunja mu msewu ndi kumuveka iye mwinjiro woyera, ndipo iwo ankamuyimika iye pa makwerero kuti mzinda wonse ukhoze kumuwona. Iwo anakonzza phwando ndi chisangalalo, ndipo bamboyo ndiye ankakhala ndi mwambo wa kumulandira. Iye ankamulandira mwana wake yemwe wa mwamuna kulowa mu malonda ake omwe, ndiyeno mwana wamwamunayo amakhala wofanana nawo bambo ake. Mwa kuyankhula kwina, ngati izo zikanakhala lero, dzina la mwana wamwamunayo pa cheke linali labwino basi monga la bambo akewo.

<sup>48</sup> Tsopano penyani chimene Mulungu anachita. Pamene Mwana Wake anabadwa, Iye anamulola Iye kuti apite kwa zaka makumi atatu, akumuyesa Iye, kumuyesa Iye. Ndiye Iye anamupatsa Iye zaka zitatu za yesero lolimba. Ndiyeno pa kutha pa yesero lolimbalo, pamene Iye anawona kuti Mwana Wake anali pa ntchito ya Atate; Phiri la Chiwalitsiro, Bukhu la Luka; Iye anamutenga Petro, Yakobo, ndi Yohane, mboni zitatu, ndipo anakwera pamwamba pa phiri, ndipo pamene Mulungu anachita malamulo a kulandiridwa. Iye. . . Iwo anayang'ana mmwamba ndipo iwo anamuwona Yesu, ndipo zovala Zake zinawala moyera ngati mphezi. Ndipo pamene Mtambo unamuphimba Iye, ndipo Liwu linatuluka kuchokera mu Mtambo, ndi kuti, “Uyu ndi Mwana Wanga wokonededwa;

mvereni inu Iye. Ine ndikhala pansi tsopano ndipo sindikhala ndi chinanso chonena. Chimene Iye anena chiri lamulo ndi Choonadi.”

<sup>49</sup> Tsopano mpingo wapyola mu masukulu amenewo. Iwo unakwatiwa mmbuyo kutaliko, nthawi yaitali kalelo, ndipo unakhala chipembedzo, bungwe. Koma, inu mukuzindikira, Kubadwa kunapereka chinthu chinachakenso. Ndipo tsopano iwo wafika pa malo pamene mpingo wa Pentekoste, ndi Kubadwa kwatsopano, wapimidwa ndi kuyesedwa, ndipo tsopano iwo ukufika pa malo . . . Mulungu samachita ndi Mpingo monga bungwe chabe. Iye samachita ndi Mpingo monga—gulu la anthu.

Iye amachita ndi Mpingo monga aliyense payekha, munthu aliyense payekha mu Mpingo. Ndipo tsopano izo zafika ku nthawi . . . Ndipo izo si chinsinsi; ife tonse tikuziwona izo. Pamene munthu akutsimikizira, ndipo Mulungu akumukonda iye, Iye amamutengera iye kunja kwinkwake kwa Iyemwini. Kumeneko pamaso pa Angelo Iye amamuchitira iye chinachake. Iye amamukwezera iye mmwamba pamenepo mu Kukhalapo kwa Mulungu, ndi kumupatsa iye mphatso, ndi kumudzazitsa iye, ndi kumukhazikitsa iye pamenepo. Ndiwo m’badwo umene ife tiri kukhalamo.

<sup>50</sup> Mzimu Woyera womwewo umene unapulumutsa Achilutera; umene unawayeretsa Amethodisti; umene unawabatiza Achipentekoste; uli tsopano kuyika mu dongosolo Kudza kwa Ambuye Yesu. Pamene, iwo uti udzakhale wamphamvu kwambiri, Thupi limenelo, lidzabwera mu Gulu ili, Mpingo, umene uti udzawako ke ena onse a iwo kuchokera mmanda. Pamenepo padzakhala chiwukitsiro. Ndicho chimene Mzimu Woyera unadzera. Kodi Mzimu Woyera ndi Chiyani? “Popanda ife iwo sangakhoze kupangidwa kukhala angwiwo.” Iwo anakhala mu tsiku lina, pansi pa izo. Ife tikukhala mu tsiku linalake.

“Pamene mdani abwera mkati ngati kusefukira, ine . . . Mzimu wa Mulungu umawutsa muyezo wotsutsa izo.” Mwaona? Ife tiri mu tsikulo tsopano . . .

<sup>51</sup> Kumbuyo uko, iwo sanali mwatheka odziwa monga lero. Iwo sakanakhoza kupanga bomba la atomiki kapena galimoto. Iwo analibe sayansi ndi zinthu monga ife tiri nazo tsopano, koma, ndi zinthu za zinthu zachinsinsi; kuti ayesere kunena kuti munthu anapemereredwera pamodzi, ndi fumbi linalake ndi zina zotero, ndi kutenga kufotokoza kwinkwake ndi kumayesera kutsimikizira izo, kuti apange anthu kukhala achikunja.

Koma tsopano, pamene ife tikuwusowa Iwo, Mzimu wa Mulungu ukuwutsa muyezo. Kodi ndi chiyani iwo? Iye akutsanulira mkati Mzimu Wake. Ndiye, iwo amene akupumula



kunja uko mu manda, kapena pansa pa guwa la Mulungu, monga Lemba limanenela, akufuula, “Mpaka liti, Ambuye? Mpaka liti? Motalikira chotani?” Mulungu akuyembekezera pa ine ndi inu. Mpingo ukuyembekezera pa ine ndi inu. Nthawi yolandiridwa, imene Mulungu akhoza kutsanulira mwa ife chidzalo Chake, Mphamvu Yake, chiwukitsiro Chake, kuti pamene Mpingo ndi Khristu zikhala pafupi chotero limodzi mpaka Khristu akhala wowoneka pakati pathu, ndi kuwukitsa akufa, ndipo ife tizipita mu Mkwatulo.

<sup>52</sup> Tsopano ife tikuti tinene, kusonyeza pakapita kanthawi, kuti iwo okha omwe adzazidwa ndi Mzimu Woyera akupita mu Mkwatulo umenewo. “Pakuti akufa ena onse sanakhale moyo kwa danga la zaka chikwi.” Ndiko kulondola. Anthu odzazidwa ndi Mzimu-Woyera okha anali onse amene anapita mu Mkwatulo. Tsopano, Mulungu anapereka Mzimu Woyera . . .

<sup>53</sup> Ine ndiri nalo Lemba lina pano, mu Yohane 14:12. Ndilo Lemba lozolowereka kwambiri ndi anthu onse pano pa kachisi.

*Indetu, indetu, ine ndikunena kwa inu, Iye amene akhulupirira pa ine . . .*

Tsopano, musati mulole liwu ilo “akhulupirira” likhale ngati lokukhumudwitsani inu. Mu mpingo mwadzina lokha, amati, “Inde, ine ndikukhulupirira. Zedi, ine ndikukhulupirira kuti Yesu Khristu ndi Mwana wa Mulungu.” Mdierekezi amakhulupirira chinthu chomwecho. Ndizo chimodzimidzi. Baibulo limati iye amatero.

Koma Lemba limati, mu Yohane, kuti, “Palibe munthu angakhoze kumutcha Yesu Khristu, kokha mwa Mzimu Woyera.” Inu muli, kwenikweni, mwa Lemba . . . Ndiroleni ine ndiyime apa miniti yokha, ndisanati ine nditsirize kuwerenga. Iwe suli wotembenuka kufikira iwe utalandira Mzimu Woyera. Ndiko kulondola.

<sup>54</sup> Iwe ukukhulupirira “kuloza.” Mzimu Woyera wayankhula kwa iwe, ndipo iwe wamuvomereza Iye poyera. Mdierekezi ali ndi chinthu chomwecho. “Ine ndikumukhulupirira Iye kuti ali Mwana wa Mulungu.” Chomwechonso amachita mdierekezi. Koma iwe ukuyendabe kupita kwa Iye.

Pamene, Petro anali atayitanidwa ndipo atalungamitsidwa, pa kukhulupirira pa Ambuye Yesu Khristu; ndipo mu Yohane 17:17, Yesu anawayeretsa iwo kupyolera mu Mawu, pakuti Mawu anali Choonadi. Ndipo Iye anali Mawu. Pa 1, Yohane amati, “Pachiyambi panali Mawu, ndipo Mawu anali ndi Mulungu, ndipo Mawu anali Mulungu. Ndipo Mawu anapangidwa thupi, ndipo anakhala pakati pathu.” Iye anali Mawu, kotero Iye anawayeretsa iwo. Iye anati, “Atate,” akuyankhula kwa Mzimu mkati mwa Iye, “Ine ndikuwayeretsa iwo kupyolera mu Mawu,” Iyemwini, pa kusanjika manja Ake pa iwo. “Mawu Anu ndiwo Choonadi.” Mwawamba chabe anamuyankhula Iye mu

kukhalapo, mu chiberekero cha mkazi; o, zosatheka kwathunthu kuti Iye akhale njira ina iliyonse kuposa Mawu awa a Mulungu kukamupanga Iye kuwonekera. “Ine ndikuwayetsa iwo.”

<sup>55</sup> Iye anawapatsa iwo mphamvu yotsutsa mizimu yosayera. Iwo anapita kunjira. Iye anayika maina awo mu Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa. Ndipo Iye anawatumiza iwo, Yohane... Mateyu 10, ndipo anawapatsa iwo mphamvu pa mizimu yosayera; kutulutsa mizimu yoyipa, ndi kuchita ntchito, ndi zina zotero. Ndipo iwo anabwerera, akusangalala, anati, “Ngakhale ziwanda zikutimvera ife.”

Iye anati, “Musati musangalale chifukwa ziwanda zikukumverani inu; koma sangalalani chifukwa maina anu ali mu Bukhu.” Ndipo Yudasani anali ndi iwo. Mukuona kuyandikira kwake momwe iye angakhoze kudza; mpaka pamwamba kupyolera mu kulungamitsidwa, kusunthira patsogolobe mpaka mu kuyetsedwa. Koma mpati pamene iye anasonyeza kuwala kwake? Mpati pamene iye anadzisonyeza yekha? Isanafike Pentekoste, iye anasonyeza mangamanga ake.

<sup>56</sup> Penyani, mzimu umenewo udzakhala wachipembedzo basi ndi wachiyeretso basi monga iwo ungakhoze kukhalira, mpaka iwo utafika kwa Mzimu Woyera, ndipo iwo adzawudula Iwo kuwuchotsapo pomwepo. Ndiwo mzimu umenewo (kodi inu simungakhoze kuwuwona iwo?) kusunthira mmwamba, wotsutsakhristu. Ndipo Yesu anati, “Iyo idzakhala yoyandikana kwambiri, mu masiku otsiriza, iwo ukanati udzanyenge Osankhidwa omwe ngati kukanatheka.” Koma, kumbukirani, ndi Osankhidwa okha omwe ati adzachiwone icho.

Mulungu amayitana mwa kusankha. Inu, kodi sindinu okondwa kuti ndinu mmodzi wa iwo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi.] Simuli inu, anthu pano usikuuno, kudziwa kuti chinachake mu mtima mwanu chikukoka, “Ine ndikufuna Mzimu Woyera umenewo. Ine ndikukufunani inu, Ambuye, mu mtima wanga”? Ndi chifukwa kuti Mulungu anayika dzina lanu pa Bukhu la Moyo wa Mwanawankhosa maziko adziko asanakhazikitsidwe. Iye ananena zimenezo.

“Palibe munthu angakhoze kudza kwa Ine,” anatero Yesu, “kupati ngati Atate Anga atamukoka iye choyamba. Ndipo onse amene adza kwa Ine, Ine ndidzawapatsa iwo Moyo Wamuyaya.” Kodi Moyo Wamuyaya ndi chiyani? Mzimu Woyera. “Moyo Wamuyaya,” tengani liwu limenelo ndi kuliyendetsa ilo mu Chigriki, ndipo ilo limati, *Zoe*. Zoe ndi Mzimu Woyera. “Onse amene Atate andipatsa Ine adzadza kwa Ine. Ndipo onse amene adza kwa Ine, Ine ndidzamupatsa iye Mzimu Woyera, ndipo ine ndidzamuwukitsa iye pa tsiku lotsiriza. Ine ndidzachita izo,” Iye anatero. Osati ayi ngati-ndi-ndi zokhudza Iwo. “Ine ndidzatero. Onse amene adza; ndipo Ine ndiwapatsa Moyo Wamuyaya.” Iye adzayenera kuti awuke, chifukwa iye ali nawo Moyo Wamuyaya.

Iye adzayenera kuti abwere. Sangakhoze kufanso ayi monga Mulungu sangakhozenso kufa.

<sup>57</sup> O, amzanga okonedwa ochokera kozungulira dziko ili ndi mu mzinda waung'ono uno, ngati ine ndikanakhoza kokha, ndi liwu langa la umunthu, kuyika mu mtima wanu kufunikira kwa kulandira ubatizo wa Mzimu Woyera, ilo likanakhala liri vumbulutso lodabwitsa kwambiri limene inu munayamba mwakhalapo nalo mu moyo wanu. Kuwona chimene...Inu muyenera kuchita izo.

Ndiroleni ine ndipange izo kumveka, zokhudza, “Ndinu wosatembenuka ayi.”

<sup>58</sup> Petro anali atapulumutsidwa. Iye anakhulupirira pa Ambuye, anamutsatira Iye. Yesu anamuza iye yemwe iye anali, anali naye iye kuti azimutsatira Iye. Iye anamupatsa iye mphanvu yotsutsa mizimu yosayera ndipo anamuyeretsa iye. Koma zitatha zonse izo, ndipo atakhala woyankhulira wamkulu wa gululo; monga Akatolika akanafunira kuzitcha izo, “bishopu wa mpingo, kapena papa,” kapena chirichonse chimene chinali, munthu wamkulu wa mpingo; komabe Yesu anati, usiku wa kuperekedwa kwake, “Kodi iwe umandikonda Ine, Petro?”

Ndipo iye anati, “Ambuye, Inu mukudziwa ine ndimakukondani Inu.”

Anati, “Zidyetsa nkhosa Zanga.” Iye ananena izo katatu.

Ndipo Petro anati, “Inu mukudziwa ine ndimakukondani Inu, mpaka ine ndidzapita ndi Inu mpaka ku—ku mapeto, ndipo ine ndidzapita nanu Inu mpaka ku imfa,” ndi zina zotero.

<sup>59</sup> Iye anati, “Tambala asanalire katatu, iwe...tambala asanalire, iwe ukhala utandikana Ine katatu.” Iye anati, “Koma, Petro, ine ndakupempherera iwe.” Mvetserani. Sindizo zonse za izo. “Ine ndakupempherera iwe. Ndipo iwe ukadzakhala utatembenuka, ndiye udzawalimbikitse abale ako.”

“Ukadzakhala iwe utatembenuka.” Iye anali atafuula. Iye mwinamwake anali atavina mu Mzimu. Iye, anali atachita mitundu yonse ya zinthu, koma iye anali asanalandire Mzimu Woyera apobe. “Ukadzakhala iwe utatembenuka, ndiye dzawalimbikitse abale ako,” ndizo zooni, “kupitiriza dongosolo Lake.”

<sup>60</sup> Tsopano ndiroleni ine nditsirize kuwerenga Yohane 14:12. Tsopano mu mutu wa 14 ndi ndime ya 12, Yesu anati, “Indetu, indetu, ine ndinena ndi inu, iye amene akhulupirira...” Ndipo iwe sungakhoze kukhulupirira... “Akhulupirira pa Ine.” Inu mukhoza kukhulupirira kwa Iye. Ndi angati akumvetsa zimenezo, nenani, “Ameni.” [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.]

<sup>61</sup> Inu mukukumbukira, mu Machitidwe 19. Ine ndikuda kuti ndilekeze izi apa, koma ine ndingoyenera kuti ndinene izo

pamene izo zikubwera kwa ine. Mu Machitidwe mutu wa 19, pamene mlaliki wa Chibaptisti uyu, yemwe anali wa-wazamalamulo ndipo anali atatembenuzidwa, ndipo iye anali akulalikira ndi kuwafikitsa anthu populumutsidwa. Ndipo iwo anali ndi chisangalalo chachikulu, akungosangalala ndi kumafuula, ali ndi msonkhano. Machitidwe 18, Akwila ndi Prisila, ife tinakamba pa izo usiku watha, ndipo iwo anali atapita kukamuwona iye. Ndipo iwo ankadziwa kuti iye anali munthu wamkulu, ndipo iye anali wophunzira. Ndipo iye anali kutsimikizira ndi Baibulo kuti Yesu anali Mwana wa Mulungu, akudziwa ubatizo wa Yohane wokha. Iye sanali kudziwa ubatizo wa Mzimu Woyera apabe. Kotero iye anati . . .

Akwila ndi Prisila, mwamuna ndi mkazache aja, opanga hema aang'ono; chomwe, Paulo anali wopanga mahema, nayenso. Ndipo iwo anali atalandira Mzimu Woyera pansu pa kuphunzitsa kwa Paulo. Iwo anati, "Ife tiri naye m'bale wamng'ono yemwe akubwera kuno. Mloleni iye ayankhule kwa ife pang'ono pokha za izo."

Ndipo pamene Paulo anabwera uko ndipo anamumva iye akulalikira, podziwa kuti iye anali munthu wamkulu, iye anati, "Kodi inu mwalandira Mzimu Woyera chikhulupirireni chanu?"

Iwo anati, "Ife sitikudziwa kuti uko . . . ngati kuli Mzimu Woyera uliwonse."

Iye anati, "Ndiye ndi kwa chiyani," kapena mawu Achigriki enieni pamenepo ndi, "inu munabatizidwa chotani?"

Iwo anati, "Ife takhala titabatizidwa kale ndi Yohane Mbatizi."

<sup>62</sup> Tsopano penyani zimene Paulo ananena. Paulo ananena, kuti, "Yohane ndithudi anabatiza kuloza ku kulapa; osati kwa kukhululukira kwa machimo, koma kuloza ku kulapa, kunena kuti, ndicho chimene inu mwachikhulupirira."

Pamene iwe ulandira Khristu ngati Mpulumutsi wakowako, iwe ukukhulupirira *kuloza* ku ubatizo wa Mzimu Woyera. Umenewo si ubatizo wa Mzimu Woyera, abale anga okonedwa Achibaptisti. Uko ndi kulakwitsa.

M'bale ananena kwa ine tsiku lina, anati, "M'bale Branham," kapena nthawi yina kale, miyezi yapitayo, iye anati, "M'bale Branham, Abrahamu anakhulupirira Mulungu, ndipo kunawerengedwa kwa iye ngati chilungamo."

Ine ndinati, "Zoonadi."

Anati, "Ndi chiyani chinanso chimene munthu angakhoze kuchita kuposa kukhulupirira?"

<sup>63</sup> Ine ndinati, "Ndizo zonse zimene munthu angakhoze kuchita. Ndizo zonse zimene iye angakhoze kuchita lero, ndiko kukhulupirira Mulungu. Koma Mulungu anamupatsa iye chisindikizo cha mdulidwe," zomwe ife tinadutsamo

usiku watha, “monga chizindikiro kuti Iye anali atalandira chikhulupiriro chake mwa Iye.” Ndipo, lero, mpaka Mulungu . . .

Iwe umakhulupirira kwa Iye pamene iwe umuvomereza Iye ngati Mpulumutsi wakowako. Koma pamene Mulungu akupatsa iwe chisindikizo cha Mzimu Woyera, Iye amakusindikizira iwe mpaka kopita kwako Kwamuyaya. Tsopano inu Abaptisti mutenge zimenezo, ndipo ine ndipita nanu inu pa chitetezero Chamuyaya. Inde, bwana. Chifukwa, “Musawukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo mpaka tsiku la chiwombolo chanu.” Inu simumasindikizidwa pa kukhulupirira kuloza, koma mumasindikizidwa ndi Mzimu Woyera. Aefeso 4:30, “Musati muwukwiyitse Mzimu Woyera wa Mulungu, umene inu munasindikizidwa nawo kufikira tsiku la chiwombolo chanu.” Umenewo umakusindikizani inu, pamene inu mupeza kukondedwa ndi Mulungu, ndipo Iye amakusindikizani inu ndi Mzimu Woyera.

Ziri chomwecho, pakuti Baibulo linati, “Palibe munthu angamutche Yesu Khristu, kupatula mwa Mzimu Woyera.”

<sup>64</sup> Inu mukuti, “Ine ndikukhulupirira izo chifukwa abusa amanena choncho.” Iwo akulondola, koma izo sizikuwerengedwera kwa inu. “Ine ndikukhulupirira izo chifukwa Mawu amanena choncho.” Ndiko kulondola, koma izo siziri za inu, zimenezo inu sizikuwerengedwera kwa inu.

Njira yokha yomwe inu mungakhoze kunena kuti Yesu ndi Khristu, ndi pamene Mzimu Woyera ubwera mwa inu ndi kuchitira umboni, ndi kudzichitira Wokha umboni, “Iyeyu ndi Mwana wa Mulungu.” Ndiyo njira yokha yomwe iwe umadziwira chiwukitsiro, ndi pamene Mzimu Woyera uchitira umboni. “Pamene Iye Mzimu Woyera abwera, Iye adzachitira umboni za Ine, kukusonyezani inu zinthu ziri nkudza; kubweretsa zinthu izi, zimene ine ndanena, ku kukumbukira kwanu.” Inu simudzazipeza izo konse mu sukulu. Mwaona? Iye adzabweretsa zinthu izi ku kukumbukira kwanu.

<sup>65</sup> Tsopano ife tikufuna kuti tiwerenge patsogolo pang’ono chabe mu Lemba ili tsopano, Yohane Woyera 14:12.

*Indetu, indetu, Ine ndinena ndi inu, Iye amene akhulupirira pa ine, ntchito zimene ine ndizichita iye adzazichita nayenso; ndipo zazikulupo . . .*

Chimene, kumasulira kolondola pamenepo ndi “zochulukira,” ngati inu mukufuna kukaziyang’ana izo.

*. . .ntchito zazikulu kuposa izi iye adzazichita; chifukwa Ine ndikupita kwa Atate.*

<sup>66</sup> Ngati Iye anapita kwa Atate, Mzimu Woyera ukanadza. Ndi kulondola kumeneko? Lemba lina linati, “Ngati ine sinditi ndichokepo, Mtonthozi sadzabwera ayi. Koma ngati Ine nditi ndichokepo, Ine ndidzabweranso ndi kudzakhala ndi inu,

ngakhale mkati mwa inu.” Mwaona, ndi Mulungu ndi inu. Pamwamba pa inu, choyamba; ndi inu, mwa Khristu; mwa inu, mwa Mzimu Woyera. Ndi Mulungu mkati mwa inu.

<sup>67</sup> Tsopano, “Ntchito zimene ine ndichita inu mudzazichita nanunso,” osati ntchito yina. Koma Mulungu akufuna kuti abweretse Mzimu Woyera, mwa inu, kuti apitirize ntchito yomweyo yomwe Iye anali kuyichita mwa Khristu.

Ntchito siyinali yofunikira kwambiri mu masiku a Lutera. Umenewo unali Mpingo wa Mulungu. Iyo siinali... Yofunikirapo pang’ono mu masiku a Wesile.

Chifukwa, “Dziko,” Baibulo linati, “lidzafookera, ndi anzerupo, ndi lauthakati mochulukira nthawi zonse.” Ife tiri... Dziko likukhala loyipa mochulukira...Ife tikudziwa zimenezo. Bwanji, munthu akuchita zinthu lero zomwe, zaka zana zapitazo sakanati aganize kuti pakanakhala anthu ankanzha chotero. “Oyipa mochulukira nthawi zonse, ndipo oyipa adzachita moyipira, nthawi zonse,” linatero Lemba, “mochulukira chulukira.”

<sup>68</sup> Kotero, Mzimu Woyera wakhala uli kusuntha. Panali kupuma kwapang’ono chabe kwa Iwo ndi Lutera; kuwuzira pang’ono kwa Iwo ndi Wesile; ndi kuwuzira kwakuyapo kwa Iwo ndi Apentekoste; tsopano mpweya ndi Mzimu zakhala zofanana. Iye akulumikizanita palimodzi, kubweretsapo kuwuzira kofanana kwa mphamvu ya Mzimu Woyera kuja monga Iye anachitira kumbuyo kuja, ali kukwaniritsa ntchito zomwezo zimene Iye anazichita kumbuyo uko, ziri kukwaniritsidwa pakali pano, chinthu chomwecho.

<sup>69</sup> Penyani chimene Yesu ananena. “Indetu, indetu Ine ndinena kwa inu, Mwana sangachite kanthu kupatula ngati Iye awona Atate akuchita izo poyamba. Chimene Atate akuchita, Iye amamusonyeza Mwana. Atate akukhala mwa Ine; Iye amachita ntchitozo.” Mwaona?

<sup>70</sup> Tsopano zindikirani, pano pali chinthu china chimene ine ndikufuna kunena pomwe apa. “Monga,” Yesu anati, “monga Atate andituma Ine. Monga,” tsopano penyani, “monga Atate andituma Ine, chomwechonso Ine ndikutumani inu.” “Monga Atate...” Kodi Atate anamutuma chotani Iye? Atate, omwe anamutuma Iye, anabwera pansu kuchokera Kumwamba ndipo ankakhala mwa Iye.

Iye anali kumapita. Iye ankati, “Ine nthawizonse ndimachita icho chimene chimawakondweretsa Atate Anga.” Mwaona? Iye anali akupita ponseponse akuchita zinthu zomwe Atate anali kumusonyeza Iye kuti achite. “Ine sindichita kanthu kupatula Atate Anga atandisonyeza Iye poyamba.” Mulungu yemwe anamutuma Iye, anali mkati mwa Iye. “Ndipo monga Atate andituma Ine, njira yomweyo Atate ananditumira Ine, chomwechonso Ine ndikukutumani inu.” Ndi chiyani

chimenecho? Mulungu mwa inu, akupitiriza (chiyani?) ntchito zomwezo, zomwezo.

Yesu anati, “A. . . iye amene *akhulupirira*, iye yemwe ali nane Ine mkati mwa iye, Mzimu Woyera; iye amene *akhulupirira*, yemwe wachitira kale umboni chiwukitsiro Changa, akudziwa kuti Ine ndiri mwa iye. Iye yemwe ali mwa Ine; ngati inu mukhala mwa Ine, Mawu Anga akakhala mwa inu.”

<sup>71</sup> Tsopano inu mukuti, “Ine ndikukhala mwa Yesu; koma ine zedi sindimakhulupirira mu machiritso Auzimu.” Izo zikusonyeza kuti Iye sali mmenemo.

<sup>72</sup> “Ine ndimakhulupirira mwa Yesu; sindikhulupirira Mzimu Woyera mu tsiku lino, osati monga iwo anali nawo Iwo kumbuyo uko.” Izo zikusonyeza kuti Iye sali mmenemo.

<sup>73</sup> Mzimu Woyera udzachitira umboni Mawu aliwonse amene Iwo unayankhula. Iye sali wabodza. Iye sachita mantha ndi aliyense kapena bungwe lililonse. Iye sasowa kusanzira munthu wina aliyense. Iye amayankhula, ndiyeno Iye amakhala ndi icho.

Ngati odzikweza, ndi osokonezeka, ndi ophunzitsidwa, kapena monga ife timazitcha izo, achuma, ngati iwo sakufuna kuti awulandire Iwo, “Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kuwutsira ana kwa Abrahamu.” Iye adzatenga azifwamba, ndi zidakhwa, ndi china chirichonsecho, ndi kuwawutsa iwo. Mulungu akhoza kuchita izo, ndipo Iye akuzichita izo. “Mulungu ndi wokhoza mwa miyala iyi kuwutsira ana kwa Abrahamu.” Winawake ayenera achite izo, chifukwa Iye ndi Mulungu.

<sup>74</sup> “Ngati inu mukhala mwa Ine, ndi Mawu Anga mwa inu, pemphani chimene inu mufuna,” chifukwa inu mukupempha Mawu Ake, ndipo Mawu Ake ndiwo Moyo. Ayankhuleni iwo. Ngati Mulungu ananena izo, ndipo inu mukutsimikiza kuti Iye ananena izo, Mzimu Woyera umachitira umboni kuti Mawu amenewo ali owona, ndiye, inu muli pamenepo, m’bale. Ayankhuleni iwo; apo izo ziri. “Nenani kwa phiri ili, ‘Sunthidwa.’ Musati mukayikire mu mtima mwanu, koma khulupirirani kuti chimene inu mwanena kuti chichitika.” [M’bale Branham akuwombetsa manja ake palimodzi katatu—Mkonzi.] Si inu amene mukuyankhula, koma Atate amene akukhala mwa inu; Iye akuchita kuyankhulako. Si inu kuyankhula kwa phiri limenelo, ndi Atate omwe ali mwa inu, akuyankhula kwa phiri limenelo. Ilo liyenera kusuntha. “Miyamba yonse ndi dziko lapansi zidzachoka,” Iye anatero, “koma Mzimu Wanga sudzatero ayi. . . kapena Mawu Anga sadzapita.” Ndithudi, Iwo sangakhoze kupita. Atate!

<sup>75</sup> Tsopano, “Ntchito zimene Ine ndichita.” Mulungu ali mu Mpingo Wake, kuti apitirize ntchito Zake. Ndicho chifukwa Iye anatomizira Mzimu Woyera. Tsopano, Iye ankadziwa izo. Iye, Iye ankadziwa kuti izo sizikanakhoza, izo sizikanakhoza kuchitidwa mwa njira imeneyo, chotero mwanjira yina, chotero

Iye amayenera kutumiza. Atate anatumiza Mwana, kuyika zonse zomwe ziri mwa kas- . . . Mwana mwa inu. Ndipo ntchito zomwezo zimene Iye ankachita, ntchito zomwe zomwezo tsopano zimene Yesu anachita, inu mudzazichita nanunso, Mpingo.

Kodi inu simukanakonda kuti muzichita ntchito za Mulungu? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Yesu anati, “Ngati inu mukufuna kuti muzichita ntchito za Mulungu, khulupirirani pa Ine.” Inu mungakhulupirire motani pa Iye? Inu simungakhoze kuchita izo mpaka inu mutalandira Mzimu Woyera.

<sup>76</sup> Chifukwa, palibe munthu angakhoze kunena kuti Iye ali Mwana wa Mulungu; inu mukunena chimene winawake ananena. “Baibulo linanena kuti Iye ali Mwana wa Mulungu; ine ndikukhulupirira Baibulo. Chabwino. “Baibulo limati Iye ali Mwana wamwamuna wa Mulungu; ine ndikulikhulupirira Baibulo. Abusa amati Iye ndi Mwana wa Mulungu; ine ndikuwakhulupirira abusa. Amayi amati Iye ndi Mwana Mulungu; ine ndikuwakhulupirira amayi. Bwenzi wanga amati Iye ndi Mwana wa Mulungu; ine ndikumukhulupirira bwenzi wanga.”

Koma njira yokha yomwe ine ndingakhoze kunena kuti Iye ali Mwana wa Mulungu, ndi pamene Mzimu Woyera ubwera mkati ndi kumachitira umboni wa Iwowokha, ndiye ine ndidziwa kuti Iye ali Mwana wa Mulungu. [M’bale Branham anagoda kana pa guwa—Mkonzi.] “Palibe munthu angakhoze kumutcha Yesu ‘Khristu,’ kupatula mwa Mzimu Woyera.”

<sup>77</sup> Ha! Palibe munthu akuyankhula mwa Mzimu wa Mulungu anamutcha Yesu wotembereredwa, kapena kunena kuti Iye anali chinachake tsiku limenelo ndi chinthu chinachake lero. Izo zimamupangitsa Iye wofooka ndi wolakwitsa. Ayi, bwana.

Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse. Mzimu woona uliwonse udzachitira umboni za zimenezo. Chabwino.

<sup>78</sup> Tsopano, Iye anati, “Ntchito izi zimene Ine ndikuchita mudzazichita inunso,” Yohane 14:12, tsopano, ntchito zomwezo.

“O,” iwo amati, “mpingo ukuchita ntchito zazikulupo lero.” Mwa njira yanji?

Iye anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita.”

“Izo,” iwo amati, “chabwino, ife tiri nawo mamishonare ponseponse pa dziko, ndizo ntchito zazikulupo.”

<sup>79</sup> Koma Iye anati, “Ntchito zimene Ine ndikuzichita.” Tsopano chitani zimenezo, chitani zimenezo poyamba, ndiye ziyankhulani za umishonare.”

<sup>80</sup> Lero, ndikuyankhula pano nthawi yina yapitayo zokhudza Achimuhamadi, iye anati, “Muhamadi anafa.”

“Ndiko kulondola, iye ali mmanda, koma tsiku lina iye adzawuka.” Iye anati, “Ngati iye atawuka kuchokera ku manda,



dziko lonse likanakhoza kudziwa izo mu maora makumi awiri ndi anai.” Iye anati, “Anthu inu mumati Yesu wakhala atawuka zaka zikwi ziwiri, ndipo palibe magawo awiri kwa atatu a anthu akudziwa izo panobe.”

Ndicho chifukwa kuti inu mumayankhula kuchokera ku mayang’anidwe a nzeru pa izo. Inu mumayankhula kuchokera pa kuyima kwa sukulu kapena maphunziro.

Ngati mpingo wonse uwu, wawukulu wa Mulungu, kuwerenga Akatolika, Achiprotestanti, onse palimodzi, akanakhala atalandira Mzimu Woyera, dziko ili bwezi likugona molimba mu Chikristu; sibwezi pali zinthu zoterozo monga chikominisi; sibwezi pali chinthu chotero ngati ndewu, kapena udani, kapena liuma, kapena udani. Yesu bwezi akukhala pa Mpandowachifumu Wake, ndipo ife bwezi tikuyenda kudutsa mparadizo a Mulungu, ndi Moyo Wamuyaya, tikukhala kwa nthawizonse; owukitsidwa kale mu thupi latsopano, tikuyenda paliponse, osadzakhala okalambanso, osadzakhalanso a imvi, osadzakhala odwalanso, osadzakhalanso a njala; tikuyenda mu zisangalalo za Ambuye, tikuyankhula ndi nyama. Ndipo, o, ndi tsiku lotani! Koma ife tachita chirichonse pambali pa chimene Iye . . .

<sup>81</sup> Iye anati, “Pitani inu ku dziko lonse ndi kukalalikira Uthenga.” Kodi Uthenga umatani? “Osati Mawu okha, koma kupyolera mu Mphamvu ndi ziwonetsero za Mzimu Woyera.” Kuwapanga Mawu a Mulungu kuwonetseredwa, ndiwo Uthenga.

<sup>82</sup> Inu simungakhoze kuchita izo. Tsopano, Yesu ankadziwa zimenezo, kuti Iye akanati azidzakhala mu Mpingo Wake.

Chotero, Iye ankadziwa kuti ife tikanadzakhala nawo masukulu aluntha. Ndipo inu simudzakhoza konse kuzipeza Izi mu sukulu ya aluntha. Iwo adzakhala ali kuzitsutsa Izo. Chifukwa, chonse chimene iwo amadziwa ndi luntha la kuphunzira kwa munthu wina, chikhulupiriro china kapena chipembedzo chimene iwo akuchifuna kuti—kuti azikhala nacho moyo. Kotero iwo—iwo amakukhazika iwe mmenemo ndi kukupanga iwo chiwalo cha thupi limenelo, ndipo, m’bale, ndikubwerezereni inu kunena zinthu zina kuchokera mu chikhulupiriro chimene chikanati chiwoneke ngati chinali changwirowo basi. “Mpingo wawukulu woyera, mayi, unapirira kumenyedwa kochuluka, iwo wapirira kukunthidwa kochuluka.” Chotero watero mdierekezi; iye wakhala akukankhidwa kuchokera kulikonse komwe iye ali, pafupifupi, ndipo iye akanali kupitirirabe chimodzimidzi basi. Inde, bwana. O, iwo adzayesa kuti abwereze kunena izi.

<sup>83</sup> Kotero Yesu anadziwa kuti padzakhala kusuntha kwa aluntha basi konga kumene kunali mu masiku Ake, mpaka pomatsuka mapoto ndi mbale, ndi kuvala zovala, ndi

kutembenzira kwina makolala, ndi chirichonse monga iwo ankachitira, zinthu zonse zosiyana izi zomwe akanati azichita. Iye anadziwa kuti iwo akanadzachita izo, kotero Iye anati, “Tsopano ingodikirani miniti. Ine sinditi ndikusiyeni inu opanda chitonthozo, Ine ndikubwera kachiwiri kuti ndidzakhale ndi inu. Chotero,” Iye anati, “ntchito zimene Ine ndizichita, inu mudzazichita nanunso.”

<sup>84</sup> Cholinga cha kutumizira Mzimu Woyera chinali kuti Mulungu apitirize kupyolera mu gulu la anthu, kuti mosalekeza aziwonetsera Mulungu kwa dziko. Ndizo chimodzimodzi. Osati mwa ka chikhulupiro, osati mwa chipembedzo; koma mwa Mphamvu ya chiwukitsiro Chake, kuwapangitsa Mawu Ake enieni; pa kutenga lonjezo Lake, ndi kuyima pa mbali ya ochepa, ndi kumukhulupirira Mulungu; ndi kupenya milengalenga yakuda ikusunthira kumbuyo, ndipo Mphamvu ya Mulungu ikusunthira mkati ndi kutenga malowo. Amen. Ndicho chimene Iye akufuna. Ndicho chimene Mzimu Woyera unatumizidwira. Ndicho cholinga chimene Iye anawutumizira Iwo. Ife tikudziwa chimene Iwo uli tsopano, ndipo ndicho chifukwa Iye anawutumiza Iwo.

<sup>85</sup> Chotero, palibe magazi ena alionse akanati ayeretse anthu. Ine sindikanakhoza kukuyeretsani inu, ndipo inu simukanakhoza kundiyeretsa ine, chifukwa ife tonse ndi obadwa kuchokera ku kugonana. Koma Yesu anabadwa popanda kugonana, ndiko kulondola, kotero Magazi Ake anali oyeretsa. Ndipo Mulungu anabwera pansu, anapanga thupi, ankakhala mu ilo, anakhetsa Magazi amenewo a kuyeretsera kwa awa, chimene mwamtheradi chinachotsa kulakwa kwa tchimo ndi manyazi. Ndiye, kupyolera mu chikhulupiro, pokhulupirira mwa Iwo, Mulungu amabwera mpaka pansu kulowa mu thupi la munthu limenelo, mwa kuyeretsa kwa Magazi amenewo, amamuyika iye Mbewu ya Abrahamu, mwa chikhulupiro.

<sup>86</sup> Kutu ukhulupirire kuti Magazi amenewo akanabwera, Magazi angwiro awo omwe akanati akhale chozizwitsa monga magazi ake, anayenda kupita kumeneko pambuyo pake “iye anali monga ngati wakufa.” Anamukhulupirira Mulungu kwa zaka makumi awiri ndi zisanu, iye wausinkhu wa zaka makumi asanu ndi awiri mphambu zisanu, ndipo iye anakhulupirira mpaka iye atafika zana. Ndipo Sarah, makumi asanu ndi amodzi mphambu zisanu, ndipo anakhulupirira mpaka iye atafika makumi asanu ndi anai. “Ndipo iye anali wina wonga ngati wakufa.”

Ndipo Mulungu anati, “Kotero kuti anthu asakhale motsimikiza kuti angachiphonye ichi, mtengere iye pamwamba apa pa phiri ndipo unkamperereke iye ngati nsembe.”

<sup>87</sup> Iye ananena kwa antchito, “Inu muyime pano ndi bulu ndipo mudikire. Mwanayu ndi ine tipita kutsidya ndi kukapembedza,

ndipo mwanayu ndi ine tikabwerera.” O, kodi iye akuti akachita motani izo?

Abrahamu anati, “Ine ndinamulandira iye ngati mmodzi wochokera kwa akufa. Ndipo ine ndikudziwa kuti Iye amene anamupereka iye kwa ine, ngati mmodzi wochokera kwa akufa, ali wokhoza kumuwukitsa iye kuchokera kwa akufa ngati ine nditangosunga kokha Mawu Ake. Kusunga, ine ndikasunga Mawu Ake; Iye ndi wokhoza kumuwukitsa iye kuchokera kwa akufa.”

<sup>88</sup> Kuyankhula mwangwiro za Khristu! Ndi Uyo apo. Ndipo kupyolera mu khungu la Magazi amenewo munachokera Mzimu Woyera, umene Iwowokha unali utamangidwa mu thupi lotchedwa Yesu. Magazi amenewo anayeretsa njira, mwa chikhulupiriro, kuti akayitane owomboledwa, kapena Osankhidwa a Mulungu. Ndipo pamene inu mwawavomereza Iwo, ndipo Mzimu Woyera utatenga kuyipidwa konse kukuchotsa mkati mwa inu, Iye amasunthira mkati momwemo, Mulungu Mwiniwake, kuti achite chifuniro Chake.

<sup>89</sup> Pansi apa, bwana woyipidwa uja ndi wokunyuka; ndipo wina wachikulire *wakuti-ndi-wakuti* uyu apa akuchita *zakuti-ndi-zakuti*; ndipo munthu wachikulire *uyu* akuyankhula za Iwo, kutsutsa Iwo. Munthu wodzazidwa ndi Mzimu Woyera adzayima kumene pamaso pa izo. Amen.

<sup>90</sup> “Ndipo iwo anazindikira. Iwo anali mbuli ndi osaphunzira, koma iwo anazindikira kuti iwo anali atakhala ndi Yesu.” Ndicho chimene Mzimu Woyera unadzera.

<sup>91</sup> Nsodzi wachikulire pang’ono sanali kukhoza kulemba dzina lake. Koma iye anayima pamenepo ndipo anati, “Kodi ife tizikhulupirira ndani, munthu kapena Mulungu?” Amen. [M’bale Branham awombetsa manja ake palimodzi kamodzi—Mkonzi.] “Lolani izo zidziwike kwa inu, ife tikanali kulalikirabe mu Dzina la Yesu.” Mai, ndi kulimba kotani! Iye ankadziwa kuti iye—iye anali ndi Nyumba kutsidya uko. Ndiko kulondola. Iye anali mwendamnjira ndi mlendo kuno. Iye anali kufunafuna Mzinda uli nkudza.

Kodi wansembe wachinyengo uja anali kutanthauza chiyani kwa iye? Iye anali pansi pa ulamuliro wa Mulungu Wakumwamba, yemwe anamuwukitsa Mwana Wake, Khristu Yesu, ndipo anamudzaza iye ndi Mzimu wa Mulungu umene unapanga miyamba ndi dziko lapansi. Ndi inu pamenepo. Iye sali kuchita mantha ndi iye. Ayi, bwana. Imfa . . .

<sup>92</sup> Bwanji, pamene iwo anamutengera Stefano wachikulire pang’ono kunj, ndipo anati, “Bweza izo!”

Iye anati, “Inu amakosi owuma, ndi osadulidwa mu mtima ndi makutu, inu nthawizonse mumakaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu anachitira, inu mukuteronso.”

Iwo anati, “Ife tikumenya iwe mpaka ufe!”

Iye anati, “Inu simukanakhoza kuchita izo ngati inu...?...”

“Ife tikusonyeza iwe ngati ife titi tichite izo kapena ayi!” Ndipo iwo anatola miyala yayikulu ndi kuyamba kumugenda iye mu mutu.

<sup>93</sup> Iye anayang’ana mmwamba, ndipo anati, “Ine ndikuwona Kumwamba kutatseguka. Ine ndikuwona makwerero akubwera pansu. Ine ndikumuwona Yesu atayima pa dzanja lamanja la Ukulu Wake.” Ndipo Baibulo silinanene kuti iye anafa; iye anagona tulo. O, mai! Ine ndikungokhoza kumuona Mngelo akubwera pansu, akumunyamula iye ndi kumamugwedeza iye ngati khanda, mayi, mpaka iye atagona tulo. O, mai! Zedi.

<sup>94</sup> Ndicho cholinga cha Mzimu Woyera. Ndicho chimene Mulungu anatumizira Mzimu Woyera. Mzimu Woyera unabwera kudzakupatsani inu Mphamvu. Ine ndiri nawo Malemba ena apa, miniti yokha. Mzimu Woyera unabwera kuti udzakupatseni inu Mphamvu. Ine—ine ndiribe... Inu mukhoza kuzipeza izi; ine ndangopita kutali kwambiri, usikuuno.

Kukupatsani inu Mphamvu, Mphamvu mu pemphero!

<sup>95</sup> Inu mumutenge munthu yemwe wakhala moyo wabwino, koma iwo nthawizonse ali ogonjetsedwa. “O, ine ndikuuzani inu...” Munthu wabwino, “O, zedi, ine ndimawakonda Ambuye, M’bale Branham.” Nthawizonse wogonjetsedwa, iwo pemphero lawo silimayankhidwa konse.

Inu mumudzaze mkazi wamng’ono uyo ndi Mzimu Woyera nthawi imodzi, muone zomwe ziti zizichitika. Pamene iye apita pamaso pa Mulungu, iye sali wogonjetsedwa. Iye amabwera molimbantima ku Mpandowachifumu wa Mulungu, akukhulupirira. Iye ali nawo ufulu chifukwa iye ali mwana wa Mulungu, mwa Kubadwa.

Mtengeni mwamuna wachichepere uyo, wamantha kwambiri, bwana amamukankha pa maloponsepo. Ati, “Dikirani miniti pano tsopano.” Chinachake chasinthu, mwaona, iye ali nawo Mzimu Woyera. Iwo umakupatsa iwe Mphamvu. Moyo wako uli wodzaza Mphamvu.

Iwo umakupatsa iwe Mphamvu mu kuyankhula.

<sup>96</sup> Bwanji, mai, anthu awo amene anali kuchita mantha, atayima kunja uko; Petro, Yakobo, Yohane, Luka, ndi ena onse a iwo. Iwo anali atafika kale mu chipinda chapamwamba, akuti, “O, ife sitingakhoze kunena kenanso. Iwo, yang’anani uko, uko kuli Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti* ndi *wakuti* kunja uko. Uko kuli Mphunzitsi *Wakuti-ndi-wakuti* ndi *wakuti*. Inu mukudziwa, iye ali ndi madigiri anai aku koleji; ife tingakayime chotani momutsutsa iye?” Petro anati, “O, ine ndikumubukira ndikumugulitsa munthu ameneyo nsomba tsiku lina. Iye, iye

anayankhula, ndipo ine sindinadziwe nkomwe chimene iye anali kuchikamba. O, ine sindikanakhoza konse kuyima momutsutsa iye.” Koma nchiyani. . .

“Ife tingakhoze kuchita chiyani, abale?”

“Iye anati, ‘Dikirani.’”

“Chabwino, ife takhala tiri kuno masiku anai.”

“Pitirizani kuyembekezera.”

“Motalika chotani?”

“Mpakana.”

“Chabwino, kodi Iye anati kuti izo zidzakhala tsiku lachisanu?”

“Iye sananene konse motalika chotani. Iye anati, ‘Mpakana.’”

Chabwino, iwo ankangopitiriza kuyembekezera. Motalika chotani? “Mpakana.” Masiku asanu ndi atatu anadutsa. “Mpakana.” Masiku asanu ndi anai anadutsa. “Mpakana.”

*Ndipo potsiriza pamene tsiku la Pentekotse linabwera kwathunthu, iwo anali onse mu malo amodzi, mwa cholinga chimodzi.*

<sup>97</sup> Mulungu anali atakhala pamwamba pa iwo, mu Mtambo wa moto; Mulungu anali atayenda nawo iwo, pa dziko lapansi; tsopano chinachakenso chinali choti chichitike. Chinachake chiri kukonzekera kuti chichitike.

*. . . iwo anali onse mu malo amodzi, mwa cholinga chimodzi.*

*Ndipo mwadzidzidzi apo panabwera mkokomo wochokera kumwamba ngati. . . mkuntho wa mphepo yamphamvu, ndipo iyo inadzaza chipinda chonse mmene iwo anali atakhala.*

*. . . malirime ogawika . . . anakhala pa . . . iwo.*

Kodi ogawika ndi chiyani? “Olekana.” Monga chibwibwi, kodi inu munayamba mwamumvapo wina akuchita chibwibwi? Iwo amati, “nha-nha-nha, o, nhu-nhu,” mwaona, iwo sangakhoze kunena kanthu. “Ogawanika, olekana.” Monga mapazi ogawanika, kutanthauza chinachake chimene “chalekana.” Iwo sanali kuyankhula. Iwo sanali kulakatula. Iwo sanali kuchita kanthu koma basi kumangopanga phokoso.

*. . . malirime ogawanika anakhala pa iwo, ngati kuti iwo unali moto. (O, iwo samakhoza kudzigwira okha!)*

*Ndipo iwo onse anali atadzazidwa ndi Mzimu Woyera, . . . Psyuu!*

<sup>98</sup> Ndiye nchiyani chinachitika? Kunja mu misewu iwo anapita. “Ali kuti Mphunzitsi uja Yonasi? Munthu amene uja ali kuti? Ndipo chiri kuti chimphona cha luntha chiya?”

“Mulungu anali pamwamba pa ife, ndi Mose, mu chisamba choyaka; Iye anatidyetsa ife ndi mana, Pamwamba. Iye anayenda ndi ife kwa zaka zitatu ndi zisanu ndi chimodzi. . . zaka zitatu ndi miyezi isanu ndi umodzi, pano pa dziko lapansi. Koma tsopano Iye ali mwa ine. Si ine amene ndikuyankhula; ndi Iye. Ine ndikudziwa yemwe Iye ali, ndipo ine ndikudziwa yemwe ine ndiri. Ine sindiri mochulukanso; Iye ali.”

Kumubweretsa iye pano! *Inu amuna aku Israeli, ndi. . . inu amene mukukhala mu Yudea, mulole ichi chidziwike kwa inu—chidziwike kwa inu, ndipo mvetserani ku liwu langa, nonse inu alaliki ndi aphunzitsi.*

Psyuu! Mai! Mphamvu ya kuyankhula! O! “Awa sali oledzera!” Kukatengera pamwamba kagulu ka ochepa kaja, zana ndi makumi awiri, kuti katsutsane ndi zikwi khumi kapena kupitirira.

*. . .awa sali oledzera, monga inu mukuganizira, powona kuti ndilo koma ora lachitatu la ora la tsiku.*

*Ndine mlaliki wa Uthenga wathunthu. Koma ichi ndi chija chimene chinayankhulidwa ndi mneneri Yoweli;*

*. . .zidzafika pochitika mu masiku otsiriza, atero Mulungu, Ine ndidzatsanulira. . . Mzimu wanga (psyuu) pa thupi lonse: ndipo anu. . . Inu munamuwona Maria kunja uko akuvina mu Mzimu, akuyankhula mu malirime ndi kumapitiriza? . . . pa thupi lonse: . . .*

*. . .ndi pa adzakazi anga Ine ndidzatsanulirapo. . . cha Mzimu wanga; . . .*

[M'bale Branham akuwombetsa manja ake palimodzi katatu.]

*. . .Ine ndidzasonyeza zizindikiro mu miyamba mmwamba, ndi. . .mu dziko lapansi pansu; . . .mizati ya moto, ndi mithuzi ya utsi:*

Mulungu anali mwa anthu Ake pamenepo. Ameni.

“Chabwino, tsopano, ndi digrii yanji imene unali nayo? Nkuti, ndi sukulu yanji komwe iwe unachokerako?”

<sup>99</sup> “Izo sizikupanga kusiyana kulikonse pakali pano.” O, iye anayamba kutsanulirapo Lembu.

*Davide anamuwoneratu iye! . . . Ambuye nthawizonse ali patsogolo panga. . . sindidzasunthidwa ayi:*

*. . .kuwonjezera apo mtima wanga unakondwera, chifukwa. . .ndipo lirime langa linapangidwitsa kukondwa;*

*. . . iye sadzasiya moyo wanga mu hade, komanso iye sadzalola Mmodzi Woyera wake kuti awone chivundi.*

*...ndiroleni ine ndiyankhule kwa inu momasuka za mbadwa Davide, ...iye ali limodzi wakufa ndi woyikidwa, ndipo manda ake ali ndi ife ... lero lino.*

Koma mwa mneneri...iye anawoneratu kudza kwa Mmodzi Wolungamayo.

*...ndipo mulole ichi chidziwike kwa inu, kuti Mulungu wamupanga Yesu uyu yemwe, amene inu munamupachika ndi manja ochimwa, limodzi Ambuye ndi Khristu. Amen!*

<sup>100</sup> “Amuna ndi abale, ife tingachite chiyani kuti tipulumutsidwe?”

*...anati, Lapani, mmodzi aliyense wa inu, ndi kubatizidwa mu dzina la Yesu Khristu kuloza ku chikhulukiro cha machimo anu, ndipo inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.*

*Pakuti lonjezano liri kwa inu, ndi kwa ana anu, ndi kwa iwo omwe ali kutali komwe, ngakhale ochulukuka monga onse amene Ambuye Mulungu wathu ati adzawayitane. Amen.*

<sup>101</sup> Malingana ngati Mulungu ali ndi anthu, Mulungu ali ndi Mpingo, Mulungu ali ndi Mzimu Woyera okwanirana ndi Iwo. Ndicho chimene Mulungu anawuperekerera Mzimu Woyera. Luntha lidzawuka; nthawizonse lakhala. Koma Mulungu ali nawo ochepa penapake. Mulungu ali nawo Mpingo waung’ono umene uti udzasunthe patsogolobe ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, kuti udzitengere Kuwala. Ndipo iwo adzakhala iwowo, kupyolera mu umboni wawo, ati adzaliweruze dziko.

Kodi Baibulo silimati Yesu anati, “Odala ali angwiro mu mtima; iwo adzamuwona Mulungu”? Ndipo kodi Ilo silimati, kuti, “Olungama, ojera, adzaweruzza dziko lapansi”? [Osonkhana, “Ameni.”—Mkonzi.] Zedi.

Umboni wanu lero udzabweretsa chiweruzo chotsutsa mzinda uno. Umboni wathu wa ubatizo wa Mzimu Woyera ndi Mphamvu ya Mulungu, moyo woyera, udzabweretsa chiweruzo chotsutsa mzindawu. Pamene ichi...

<sup>102</sup> “Iwo omwe ali oyamba adzakhala otsiriza; iwo omwe ali otsiriza adzakhala oyamba.” Ine sindidzadziwa kanthu za Sankey ndi Moody, mu chiwukitsiro chawo. Iwo sadzadziwa kanthu za ine, mu ichi. Koma ine ndidzayima mu ichi, kuti ndipereke umboni; choteronso inu mudzachita.

Ndipo kupyolera mu iwo, mwa kumwaza kwa Kuwala kwanu, ndi ubatizo wa Mzimu Woyera, ndi mwa miyoyo yomwe inuyo munakhala, ndi zinthu zomwe Mulungu wazichita kuti atsimikizire kuti Iye akusuntha pano; ndipo ndi luntha lawo, anayenda kupita kutali ndi Icho; iwo adzaweruzidwa ndi ojera. Iwo aweruzidwa kale. Iwo achidutsa kale icho. O, mai!

<sup>103</sup> Ine ndinali kuyankhula pa Mphamvu ya pemphero, Mphamvu ya kuyankhula, Mphamvu ya moyo wopatulika. Amen. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli woti uchite.

<sup>104</sup> Ena a inu anthu mumayenda motsatira, nkumati, “Chabwino, ine sindingakhoze basi kuleka kumwa. Ine sindingakhoze basi kuleka *izi*.”

Mzimu Woyera umabwera kuti udzakhale mwa inu, kuti udzapange zonse izi “zosakhozekazi” kupita kutali ndi inu. Ndiko kulondola. Kuwapanga akazi kusiya kudula tsitsi lawo, kuwapanga iwo kusiya kuvala akabudula ndi zomasula. Popanda zowiringula. Kuwapanga iwo kusiya kulongolola. O, inde, ndicho chimene Iwo umadzera, kuti ukupangeni inu amoyo wopatulika. Iwo udzatsatira Malangizo a Baibulo nthawi iliyonse.

<sup>105</sup> Mkazi akati, “Kwathenta kwambiri basi; ine ndikungoyenera kuti ndivale izi. Zimandimvetsa ine mutu ngati ndizilola tsitsi langa kukula.”

Koma palibe zowilungula ndi Mzimu Woyera. Iwo uli pamenepo kuti upangitse izo kutero. Iwo uzitsatira Mawu chimodzimodzi basi. Ndizo zomwe Mzimu Woyera uli woti uzichita.

Ndi woti uzikupangani inu amuna kupotoloza mutu wanu kuchokera kwa akazi ovala mwatheka awo, ndi kuleka kuwakhumbira iwo, ndiwo ziwalo za mpingo. Ndizo zomwe Iwo uli woti uzichita.

<sup>106</sup> Ndi kuti uletse chokupangitsani inu kusuta ndi kumwa, ndi kukhala...kufuna kukhala khutchu. Iwo udzachotsa izo mwa inu. Iwo udzakuchepetsani inu pamene inu mukuchita izo. Ndizo zomwe Mzimu Woyera unaperekedwera. Ndi wa moyo wopatulika. Ndiko kulondola. Kukupangitsani inu kusiya miseche. Kukupangitsani inu kusiya kusewera njuga, kuponya daisi, ndi zinthu zina zonse izi zimene inu mumachita paseri pa ngodya.

Iwo udzakupangitsani inu kusiya kumapitiriza momwe inu mukuchitira, kukhala moyo wosawona kwa akazi anu. Ndicho chimene Iwo uti udzachite. Ndiko kulondola. Iwo udzakusiyitsani inu kufuna kukwatira mkazi wa munthu wina. Ndiko kulondola chimodzimodzi.

Ndicho chimene Iwo uli. Ndi woti ukupangitseni inu kumakhala moyo wopatulika. Ndicho chimene Mzimu Woyera uli Mphamvu yake, “kuti iyike zokhumba zanu pa zinthu Zakumwamba,” kumene Mulungu akuyima pa...?. . .lingaliro la Khristu mwa inu. Inu simungadziletse kuziwona zinthu zimenezo; pamene inu muyang’ana pa izo, inu muzipotoloza mutu wanu. Ndiko kulondola. Ndi woti uzikupangitsani inu.



<sup>107</sup> Inu mukuti, “Ine sindingakhoze kuchita izo. O, ine sindingakhoze basi kuchita zimenezo.” Zedi, *inu* simungakhoze.

Koma Mzimu Woyera unadzera cholinga chimenecho. Ndicho chimene Iwo unachita. Iwo unabwera kuti udzachotse izo mwa inu, zizolowezi zonse zakale izo ndi zinthu zomwe inu mukuzichita.

Miseche yakale ija, kudzipatula nokha, kumati, “Mulungu adalitsike, ndine wa Methodist, ine sindingakhale nako kanthu kochita ndi oyera-odzigudubuza akale aja.” Mzimu Woyera unabwera kuti udzachotse izo mwa inu.

<sup>108</sup> “Ndine wa Baptisti. Ndine wa Presbateria. Ine sindingapite ku gulu laling’ono lija lachikale la oyera-odzigudubuza.” Mzimu Woyera unabwera kuti udzachotse kukhuthara konse uko mwa inu. Ndicho chimene Iwo unachita. Iwo umakutsukani inu mu Magazi; kukusitani inu bwino. Ndicho chimene Iwo unadzera kuti udzachite.

Iwo unabwera kuti udzakuwongoleni inu bwino. Iye anati, “Konzani malo okhota awongoke.” Ndicho chimene Iwo unadzera kuti udzachite; kuziwongola izo. “Kupanga malo okwera kutsika; kupanga mapiri onse kuwoneka ngati kuti onse akuvina ndi monga tinkhosa tating’ono, ndi masamba onse akuwombera manja awo, kwa inu.” [M’bale Branham anawombetsa manja ake palimodzi kanai—Mkonzi.] Mbalame kumayimba mosiyana. Mabelu achisangalalo akulira. Palibepo zowiringula ayi. Ndicho chimene Iwo unadzera kuti udzachite. Ndicho cholinga cha Mulungu potumiza Mzimu Woyera, koteri inu mukanati muzichita zinthu izi, kuti inu mukanati muzichita ntchito . . . kuyenda motsatira Iye.

<sup>109</sup> Tsopano ine sindikufuna kuti ndikuvulazeni inu, koma ine ndinakuwuzani inu kuti ine ndiri pano ndi kuya kwa koonamtima. Kutu ndisati ndikutsinani inu, kamodzi pa nthawi ine ndikumalumpha kuchoka pa mzere penapake; ndi kukhala ndi Choonadi, koma kukhala pamenepo ndi kuzipanga izo mwanjira yakuti izo zisati zikutsinani inu molimba kwambiri.

<sup>110</sup> Koma ine ndikufuna kuti ndikuuzeni inu chinachake. Ngati Baibulo likunena kuti ndi kolakwika kuti mkazi azidula tsitsi lake, ndipo inu nkumati muli nawo Mzimu Woyera ndiyeno mukumadula tsitsi lanu, ine ndikudabwa ngati inu muli nawo. Musati muchite misala; ngati izo zikutero, izo zikusonyeza panobe kuti pali chilemba china chokutsutsani inu.

<sup>111</sup> Ngati Baibulo likunena kuti nkolakwika kuti mkazi azivala chovala chomwe chiri cha mwamuna, ndipo inu mukumavala maovololo akale awa ndi zazifupi kunjira kuno pa msewu, inu akazi achikulire! Ndikuganiza mwana wamng’ono akanakhala yense . . . ujeni, kuti azisewera ndi anyamata aang’ono ndi zinthu. Koma, penyani, pamene inu—pamene inu akazi achikulire, a zaka khumi ndi zisanu, khumi ndi zisanu ndi

chimodzi, khumi ndi zisanu ndi zitatu zakubadwa, mpaka kwa agogo, kunja uko pa msewu! Ndipo Baibulo linati, “Ndi themberero mu maso a Mulungu,” kwa mkazi kuti avale zinthu zimenezo. Ndipo inu mumavala izo, mulimonse, ndipo nkumati inu muli nawo Mzimu Woyera? Ine ndimadabwa nthawizina. Mzimu Woyera ungatsatire Mawu a Mulungu mpaka ku lemba.

Ndipo mlaliki paseri pa guwa, yemwe alibe chisomo chokwanira kuti alalikire Iwo, ine ndikukayika ngati iye ali nawo Iwo. Ndiko kulondola chimodzimodzi basi! Chabwino, ndicho chimene Mzimu Woyera unadzera.

<sup>112</sup> Ndi woti umupatse mlaliki kulimbika. Ndi woti upereke chiyero kwa gulu. Ndi woti ukhazikitse Mpingo mu dongosolo. Ndi woti ubweretse umodzi wa Mzimu. Ndi woti utiyanjanitse ife palimodzi ndi Mphamvu. Ndiwo kuti utiyanjanitse ife palimodzi ndi chikondi, chikondi chapaubale.

Ine sindikusamala ngati ndinu wa Methodisti, Baptisti, Presbateria, Chilutera, chirichonse chimene inu muli, ngati ife tonse takhala mwa Mzimu Woyera umodzi titabatizidwira kulowa mu Thupi limodzi, ndi kukhala ziwalo za Thupi la Yesu Khristu. Palibe ayi...palibe chimene chiripo, palibe chamtsogolo; njala, chilala; palibe chimene chingatilekanitse ife kuchoka ku chikondi cha Mulungu, chikondi cha Khristu, “chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu,” chifukwa ife ndife obadwa ndi Mzimu Wake, otsukidwa mu Magazi Ake. Iye ndife cholengedwa chatsopano. Ndicho chimene Mulungu anadzera kuti adzachite. Ndicho chimene Mzimu Woyera unadzera. Inde, bwana. Nchonwe chiri.

<sup>113</sup> Tsopano, anthu, yang’anani kwa ine, mu nkhope. Manja ambiri anakwera mmwamba, omwe munali nawo Mzimu Woyera; mwaona, zedi, iwo analipo. O, tsopano ndati—ndati ndingotuluka pang’ono pokha apa. Izi zikujambulidwa. Koma ife tikuti titenge zambiri za izo mawa usiku.

Ngati inu mukuti inu muli nawo Iwo, ndipo ndinu wolakwa pa izi, ine ndikudabwa chimene chiri kukutsogolerani inu. Mulungu sangakutsogolerani inu konse kuchoka pa Mawu. Iye adzakusungani inu limodzi ndi Mawu, chifukwa ndiwo malamulo Akeake a Mulungu, a Mpingo Wake, kwa anthu Ake, kwa akazi, ndi kwa amuna.

<sup>114</sup> “Chabwino,” mukuti, “izo siziri kundipweteka ine pochita izi kapena izo.” Izo sizitero? Mawu amati izo zimatero.

Ndipo ngati Mzimu Woyera uli mwa inu, Iwo udzakutsogolerani inu mpaka ku Mawu. Pamenepo sipakhala pali zowiringula ayi. Mulungu samapanga zosinthitsa kapena zowiringula. Iye amapanga chilemba ndipo inu muponde pa icho. Ndizo zonse. Ndicho chimene chiri ndi aliyense. Inu mumabwera njira yomweyo.

115 Petro anati, “Lapani, mmodzi aliyense wa inu; mukhale obatizidwa, mmodzi aliyense wa inu, mu Dzina la Yesu Khristu kwa kukhululukiridwa kwa machimo anu, ndiye inu mudzalandira mphatso ya Mzimu Woyera.” Mwaona? Ndi zimenezo. Ife tiyenera kugunda mzere umenewo.

116 Tsopano ine sindikutanthauza kuti ndikupwetekeni inu; ine ndimakukondani inu mochulukwa kwambiri. Koma, m’bale, mlongo, kodi inu mukuzindikira, ndi . . .kuti ine ndikudziwa kuti ine ndikuyenera kuti ndidzayime mu masiku otsiriza pa chiwukitsiro chimenecho, ndi m’badwo uno wa anthu, ndi kupereka chofotokoza chifukwa cha Mawu awa? Ndipo Mzimu Woyera ukusonyeza izi, ndipo ine ndikuwalalikirira Iwo kutali, kodi inu mudzakayima pati? Kodi iwe ukadutsa nazo chotani izo? Iwe sungakhoze kuchita izo, mzanga. Usatero. Tsopano siyani izo. Chirichonse chimene inu mukuchita chimene chiri cholakwika, chisiyeni icho.

Inu mukuti, “Ine sindingathe.”

Ndiye inu mulibe Chokhozetsa mwa inu panobe. Pamene Mzimu Woyera ubwera, Iwo umakupatsani inu Mphamvu pamwamba pa dziko. Ndipo ngati inu . . .Mvetserani chimene Iye ananena. “Ngati inu mulikonda dziko kapena zinthu za mdziko, ndi chifukwa chikondi cha Mulungu sichiri mwa inu.” Tsopano, palibe zowiringula. Iye amazipangitsa izo kumveka, ndipo ife tiyenera kubwera mpaka pa mzere umenewo.

117 Ine ndikudziwa inu mukuganiza kuti ndine waukali. Koma ine ndangokhala ndazaza kwambiri pakali pano. Mwaona? Mvetserani. Izo ndi zoono. Tsopano bwerani mpaka kwa Iwo, m’bale, mlongo.

118 Musati mulole ena a makoleji aluntha kozungulira kuno akuwuzeni inu kuti, “O, ndizo zinthu zachikale zautsi.”

Ngati Iwo uli chinthu chakale chautsi, ndiye Mulungu ndi wakale wautsi. Ndipo ngati Mulungu ali wakale wautsi, ndiye ine ndiri, nanenso. Amen. Ine ndikufuna kuti ndikhale monga Iye. Chifukwa chiyani? Mzimu Wake uli mwa ine, umene ukumamva njala ndi ludzu, kuchitchula chirichonse chosiyana ndi Mawu . . .

119 Ngati anthu akuti, “Ndi zabwinobe kuti, o, kuti munthu aziseweretsa makadi aang’ono podzisangalatsa, ndi kumangochita njuga ndi koloni kapena ziwiri. Zonse ndi zabwino.” Mulungu akuti si zabwino.

120 “O, ngati iwe ungotenga chakumwa chosangalatsa, ndi kumangokhala wolezera pang’ono, kamodzi mu kanthawi.”

Koma Mulungu akuti, “Tsoka kwa iye.”

121 “O,” inu mukuti, “zonse ndi zabwino, M’bale Branham. Ine—ine—ine ndimadula tsitsi langa chifukwa cha chinthu chenicheni. Mkazi, inu mukudziwa, akazi ena onse amachita

zimenezo.” Ine sindikusamala zimene akazi ena akuchita. Iwo sali chitsanzo chanu kapena iwo sali bwana wanu. Ngati inu muli nawo Mzimu Woyera mwa inu, inu muzitsatira malangizo Ake mosasamala zimene anthu akunena za inu.

<sup>122</sup> “Chabwino, M’bale Branham, kwangokhala kotentha kwambiri, ndipo ine ndinangoyenera kuvala zovala izi zazing’ono *zakuti-ndi-zakuti*.” Gehena ndi wotentha kuposa zimenezo, mlongo wokondedwa. Ndiroleni ine ndikuwuzeni inu zimenezo. Ndipo—ndipo musati. Inu muzikumbukira zimenezo.

<sup>123</sup> Ndipo Mzimu Woyera nthawizonse udzakutsogolerani inu ku Choonadi, ndipo Choonadi Chake ndicho Mawu. “Mawu Anga ali Choonadi. Mulole mawu a munthu aliyense akhale bodza, koma mulole anga akhale owona.”

Ndipo tanganzani, “themberero.” Kodi inu mukanakhoza kuganiza?

<sup>124</sup> Awa ndi mawu oyipa kuti mtumiki awanene, koma ine ndapita mu zimbudzi mu malo momwe mumangokhala... Iwe umayenera kuti uyende kutuluka chobwerera, pafupifupi izo zimangokhala basi...Ndi zinthu zonyansa pa khoma. Ine ndinaganiza, “Ndi motani mdzikomu momwe anthu angakhale otsika pansi chotero?” Ndi kununkha! Ndipo pamene ine ndiyenda kulowa mu malo amenewo, ine kawirikawiri ndaganiza, “Kununkha kotani!” Ine ndima...Mmenemo, ine ndimachita kugwira mphuno yanga monga *chonchi*, potsuka manja anga. Ine ndimachita mantha kuti pamene ine nditi ndigwire chotsegulira chitseko, kachiwiri, pangakhale majelemusi ochokera ku zindoko ndi zinthu. Ndipo ine ndinaganiza, “O!”

<sup>125</sup> Tsiku lina, nditayima pa bwalo la ndege, ena a malo awo amene ine ndinayendamo, kapena malo a njanji, ine ndinayenda kulowa mmenemo. Ndipo ine ndinaganiza, “O, chifundo.”

<sup>126</sup> Ndipo Chinachake chinanena kwa ine, “Ndi momwe dziko limanunkhira kwa Mulungu. Ndi themberero.”

<sup>127</sup> Ine ndinaganiza, pamene ine ndimuwona mkazi akuyenda pansu mu msewu, ndipo yense atadzinyamulira kunja monga choncho, ndipo atavala zovala zachimuna, ndi momwe izo zimawonekera kwa Mulungu. Ndizo themberero, chinachake chimene chiri chonyansa ndi chonunkha, pamaso pa Mulungu. Komabe, iye adzapita ku tchalitchi Lamlungu, ndipo atadzikongoletsa.

Uko kumapita amuna kumeneko, ndipo amamwa, ndi kunama, ndi kukonda ndalama, ndi kumunamiza woyandikana naye nyumba, ndi china chiri chonsecho, kuti apeze ndalama zina zowonjezera; ndi kuchita zinthu izi, ndi kuchita njuga, ndi kusuta, ndi kumwa, ndi kunama; ndiyeno nkumapita ku mpingo ndi kukachitira umboni. Themberero! Nyansi! Ndiwo mpingo waluntha.

128 Kumati, “Chabwino, ine ndine wa mpingo.” Inde, ndipo nkumachita kuulola mpingo utuluke, maminiti khumi ndi asanu, kotero madikoni onse ndi onse a iwo akhoza kukasuta, ndi abusa, nawonso, asanati akakhalenso ndi mpingo. Ndiuzeni ine? Dzipatuleni nokha kuchoka ku chinthu chosayera chirichonse!

129 “Liyipitse thupi; ine ndidzaliphwasula ilo.” Mulungu anati Iye adzachita izo. Ndipo lero, pa khansara, iyo ikupangitsa magawo asanu ndi anai ndi china a imfa, za khansara wa kummero ndi mapapo, amayambitsidwa pa kusuta fodya. “Liyipitse thupi; ine ndidzaliphwasula ilo.” Koma iwo ali omka ku gehena, kumadzigudubuza monga choncho, iwo sakudziwa.

Ndipo mlaliki wina atayima mu guwa ndi madigiriri anai, atachokera ku koleji, akusuta, iyemwini. Ndiroleni ine ndikuuzeni inu chinachake, m'bale. Mzimu Woyera unatumizidwa kuti udzayitane amuna ndi akazi kuchoka ku chinthu chimenecho. Dzipatuleni nokha!

Mawu oti *mpingo* amatanthauza kukhala “wolekanitsidwa.” “Tulukani kuchokera pakati pa iwo,” linatero Baibulo. “Musakhudze ayi zosayera zawo, ndipo Ine ndidzakulandirani inu; ndipo inu mudzakhala ana aamuna ndi aakazi kwa Ine, ndipo ine ndidzakhala Mulungu kwa inu.” O, mai! Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wankhanza, koma ine ndikutanthauza kuti ndikhale woonamtima ndi kuti ndikhale wooka kwambiri. Inde, bwana. O, ndi chinthu choyipa bwanji!

130 Amuna ndi akazi, kodi ife tayima pati lero? Kodi ife tiri pati? Tiyeni tiyime.

131 Usiku wina, pa mpando waung'ono wakale apo mu chipinda, (ndipo ine ndiyenera kutseka), mpando wakale waung'ono wantchito pawiri. Nditatha kupemphera kwa masiku atatu kapena anai, chotero ine ndinafika mu malo oterowo, kupita chozungulira, ndi kumaganiza, “O Mulungu,” ndipo ine ndinafika mu malo otero mpaka ine sindinali kudziwa choti nkuchita. Ine ndinati, “Mulungu, ife tiri pa mapeto a msewu. Ndipo ine ndikuzindikira kuti ine ndanyalanyaza. Ine ndakhala nako kuyitana koti ndizipitirira patsogolo, ndipo nkukhala wotopa, ndi kusakhoza kuchita izo.” Ine ndinaganiza ndiye ine ndimakhoza kuwawona Ambuye anga akuzandima kupyola mu mdima kutali, pamene Iye anali wotopa kwambiri Iye amalephera ngakhale kutukula phazi limodzi kutsatira limzake linalo, koma Iye sanali nayenso... Anamuyimira mkazi waku Naini, kenako mnyamata yemwe anabweretsedwa kumeneko yemwe anali wakufa; mpaka Iye anapita ndipo anakhudza machira, ndi kugwiritsa ntchito mphamvu zocheza zimene zinali mwa Iye kuti amuwukitse mnyamata ameneyo. “Chabwino, ine ndimakhala wotopa chotani? Chavuta ndi chiyani ndi ine, Ambuye? Pano ine ndikugaganiza, ‘Chabwino, ine ndikuyamba kukalamba. Ine—ine sindingakhoze kuchita izo’”

<sup>132</sup> Apo panali Mose, Mulungu yemwe uja yemwe ine ndikumutumikira, ankayima uko, usinkhu wa zaka zana ndi makumi awiri.

Uko kunali Kalebu, yemwe ankayima usinkhu wa makumi asanu ndi anai, ali ndi lupanga mu dzanja lake, ndipo anati, “Yoswa anayika lupanga ili mu dzanja langa, zaka makumi anai zapitazo.” Iye anali makumi asanu ndi atatu pamenepo. Anati, “Ndine mwamuna lero basi monga ine ndinaliri panthawiyo.” Amen.

Ine ndinati, “Mulungu, khalani achifundo kwa ine.”

<sup>133</sup> Ine ndinati, “Chabwino, yang’ana apa, ndiri nthawizonse. . .” Ndipo ine ndinamutenga mkazi wanga (kuseri uko) pa dzanja, pamwamba pa Baibulo ili ndi Baibulo lake laling’ono, ndipo ine ndinati, “Wokonedwa, ine ndakhala wotsutsa kwambiri. Mzimu Woyera ukunditsutsa ine mkati mwanga.” Ine ndinati, “Ine ndikuganiza za agologolo aja kutsidya kuja. Ine ndikuganiza za Hattie Wright kuseri uko, ndi anyamata aang’ono. Ine ndikuganiza za chimene Mulungu anachita, kusonyeza kuti Iye anali Mulungu, yemwe akanakhoza kulenga.” Aleluya!

Ine ndinaganiza, “Iye anandiiza ine izo, zaka zapitazo, ‘Ine sindidzakusiya iwe. Ine sindidzakutaya iwe konse. Palibe munthu ati adzayime pamaso pa iwe, masiku onse a moyo wako. Ine ndidzakhala ndi iwe. Ndipo kuchokera pa dzanja ili la kuzindikira za mumtima, izo zidzafika mpaka iwe uzidzadziwa chinsinsi cha mtima. Zikadzachitika zimenezo, izo zidzakwerera kwerera.’ Chaka zitachitika izo, atatsimikizira mwangwiwo, kuzungulira dziko. Apa pakubwera uwu, utumiki wina wawukulu uwu, patali kupitirira uwo.”

Ine ndinati, “Wokonedwa, ine ndikutenga dzanja lako. Mwa kuthandiza kwa Mulungu ndi chisomo cha Mulungu, asandirole ine kuti ndikhale wotsutsa kachiwiri. Andirole ine ndiyende nacho ku chitsitsimutso ichi kuno kuti ndikalalikire mosafanana ndi kale lonse. Ndiroleni ine ndipite kuno, kuti poyamba ndikadziyeretse ndekha, ndi kuwapangira anthu njira; kuti machimo anga omwe, kulekerera kwanga komwe kukhale pansu pa Magazi, zoperewera zanga zomwe zikhale pansu pa Magazi, kuti ine ndikakhoze kuyenda panja ndi kukati, ‘Nditsateni ine, anthu.’” Ndiko kulondola.

Ine ndimadana nazo kumuwona munthu akuti, “Inu mupite mukachite izo.” Ine ndimakonda kumuwona winawake yemwe angatsogolere njira kuti achite izo. Inde, bwana.

<sup>134</sup> Kuno nthawiyina kale, ife tinali ndi moto kumusi mu mzinda kuno, Kampani ya Mafuta ya Pfau inagwira moto. Iwo anayitana Dipatimenti ya Moto ya Jeffersonville kumusi uko. Ndipo mzanga wa ine, munthu wabwino, anali asanazolowere moto waukulu ngati umenewo, iye anali kuyenda kumeneko,

akuti, “Wazani madzi pang’ono cha *apa*, anyamata. Wazani madzi pang’ono cha *apa*.”

Parabwera waku Clarksville wamng’ono pamwamba apo, “ngiri, ngiri, ngiri, ngiri,” kuthamangira kumtunda uko. Ndipo iye anati, wamkulu wa amoto analumphapo, nati, “Wazirani madzi pang’ono pansi *pano*. Gwetsani zenera ili *apa*. Wazirani madzi pang’ono *pamenepo*.”

<sup>135</sup> Koma kuwoloka mtsinjewo kunabwera amuna amoto ophunzitsidwa ochokera ku Louisville. Chimbeza chachikulu chija ndi makwerero asanayime konse mkuluyo anali ali pamapeto a makwererowo. Pamene makwererowo anali kukwera, iye anali ali patsogolo. Anaponya nkhwangwa yake iye asanakafike pamenepo, ndipo analigwetsa zeneralo, anati, “Zibwerani, anyamata!” Ndi choncho. Motowo unazima mu maminiti pang’ono.

Osati, “Wazirani madzi pang’ono *apa*. Wazirani madzi pang’ono *apo*.” Zikukuikirani mu malingaliro, ena mwa alaliki aluntha awa.

<sup>136</sup> Zibwerani motsatira! Tiyeni tizipita! Ine ndikudziwa Icho ndi Choonadi. Ine ndachilawa ndipo ndachiwona. Ulemerero! Mzimu Woyera ndi wolondola. Mulungu ndi wabwino. Musamati muziyesera *apa*, kuyesera *apo*; tiyeni tiyende kulowa mwa Iye! Iye ali pano. Ndi wa inu. Mulungu anapereka Mphamvu Yake kwa Mpingo Wake. Osati wazirani *izi* apa, ndi wazirani apo; inu simudzapeza kalikonse katachitika. Pitani patsogolo! Ameni. Nhu! Psyuu!

Sindikukhozanso ngakhale kupenya kupyolera mwa iwo. [M’bale Branham akuchotsa magalasi ake owerengera—Mkonzi.]

<sup>137</sup> Ameni! Kodi ife tichita chiyani? Munthu aliyense yemwe wakhala pano ali wodzazidwa ndi chinachake.

Ndiye ine nditseka; ndiyenera kutero, zikatha izo.

Ndinu wodzazidwa ndi chinachake. Inu simungakhoze kukhala pamenepo wopanda kudzazidwa ndi chinachake. Inu muli nawo moyo mwa inu. Moyo umenewo umakulamulirani inu, ndipo moyo umenewo ukulamuliridwa ndi mzimu.

Tsopano, inu mukhoza kukhala odzazidwa ndi dziko, kulikonda dziko kapena zinthu za mdziko. Mulungu akhale wa chifundo kwa inu.

Inu mukhoza kukhala wodzaza tizikhulupiro ta ku mpingo winawake, pemphero lina laling’ono lomwe inu mumanena, inu mukuganiza kuti ilo lipempherera kwa munthu winawake wakufa, kapena—kapena kupanga mtundu winawake wa chizindikiro mwamtanda pa inu. Mulungu akhale wachifundo kwa inu.

<sup>138</sup> Ndipo inu mukhoza kukhala wodzaza chipembedzo, ndipo izo nzoyipa aponso. Ndiko kulondola. Ndiko kulondola. Baibulo linati, “Mu masiku otsiriza iwo adzakhala achipembedzo kwambiri, okhala nawo mawonekedwe aumulungu; okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yakeyo: kwa oterowo chokaniko.”

Ngati inu muli wodzaza ndi chipembedzo, ndinu omvetsa chisoni; chipembedzo chokha, ndizo zonse. Ngati ndinu wodzaza tizikhulupiriro, inu simukudziwa za chimene inu mukuchikamba. Ngati muli wodzaza dziko, ndinu wakhungu.

<sup>139</sup> Ndiyeno, kachiwiri, inu mukhoza kukhala wodzaza ndi Mzimu Woyera. Amen. Ine ndikuyembekeza inu muli. Ndipo, ngati inu simuli, ine ndikuyembekeza mufika podzaza. Ndipo ngati muli odzaza ndi Mzimu Woyera, inu muli ndi chiyani? Inu muli ndi Mphamvu. Inu muli ndi chikondi. Inu muli nawo mtendere. “Mtendere Wanga ine ndiwupereka kwa inu; osati monga dziko, Ine ndikupatsani inu.” Inu muli nawo mtendere. Inu mwasindikizidwa. Inu muli nacho chizindikiro. Amen. Inu muli nawo mpumulo. Inu muli nacho chimwemwe chosaneneka, ndipo chodzaza ulemerero. Inu mwazikika. O, mai! Ndicho chimene inu muli, ndi Mzimu Woyera. Inu muli. . . Ngati inu muli wodzaza ndi Mzimu Woyera, “Inu mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo,” kuyembekezera chiwukitsiro cha aliyense mu tsiku lotsiriza. Amen!

<sup>140</sup> Mu dziko lomwe likudza, kupyolera mwa Ambuye wathu Yesu Khristu, ndi iwo amene amuwona Iye akubwera mu ulemerero ndi ukulu, “Nyanja idzapereka akufa ake.” “Matupi achivundi a iwo ogona mwa Iye adza. . .”

“Ogona mwa Iye.” Kodi inu mumalowa chotani mwa Iye? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwira kulowa mu Thupi limodzi.”

“Matupi achivundi a iwo omwe anagona mwa Iye adzasinthidwa ndi kupangidwa monga thupi Lake Lomwe la ulemerero, pamene Iye ali wokhoza kugonjetsera zinthu zonse kwa Iyemwini.”

“Ine ndinamva liwu kuchokera Kumwamba,” anatero Yohane, “linati kwa ine, ‘Lemba, “Odala ali akufa omwe afa mwa Ambuye. . .”” Inu mukalowamo chotani mkati? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi.” [M’bale Branham akuwombetsa manja ake limodzi kamodzi—Mkonzi.] “ ‘ . . . amene afa mwa Ambuye kuchokera pano mpakana; pakuti iwo amapuma ku ntchito zawo; ndipo ntchito zawo zimawatsatira iwo.” ” Nhu!

Ndicho chomwe Iye anatumizira Mzimu Woyera. O, chitsimikizo chodala, Yesu ndi wanga! Ine ndiri mwa Iye, ndipo Iye ali mwa ine; Atate mwa Iye, ndipo Iye mwa Atate; ndipo Atate mwa ine, ndi ine mwa Iye.



Yesu ndi wanga!  
 O, ndi kulawiratu kotani kwa ulemerero  
 Wauzimu!  
 Ndine wolowa wa chipulumutso, wogulidwa  
 ndi Mulungu,  
 Wobadwa ndi Mzimu Wake, pamene  
 ndatsukidwa mu Magazi Ake.

Ameni. Ine sindikanakhoza kusinthanitsa icho. O, mai!

Miyala yonse ndi daimondi, ndi siliva ndi  
 golide,  
 Nkhokwe Zake ziri zodzaza, Iye ali nacho  
 chuma chosaneneka.

Pakuti ndine mwana wa Mfumu!  
 Ine ndine mwana wa Mfumu!  
 Ndi Yesu Mpulumutsi wanga,  
 Zikundipanga ine mwana wa Mfumu!

<sup>141</sup> Ameni ndi ameni. Ine sindingakhoze kusinthanitsa izo. Ine sindingakhoze kusinthanitsa izo. Ine ndiri nawo Malemba ena awiri kapena atatu. . .

Ndiye, pano pali Lemba lina. Pamene—pamene iwe uli wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndizo zinthu zimene iwe uli nazo. Ndiye ndiwe yani, kwa dziko? Mlendo. Ine ndikudziwa tachedwa, koma sitinachedwe kwambiri kwa izi. [M'bale Branham akuwombetsa manja ake limodzi kamodzi—Mkonzi.] Mlendo! O!

Ndife amwendamnjira ndipo ndife alendo  
 kuno,  
 Ife tikufunafuna mzinda wakudza,  
 Bwato la moyo posachedwa likudza,  
 Kudzasonkhanitsira Ngale Zake Kwawo.

<sup>142</sup> Ine ndikukhoza kuwamva madzi akukhavukira kutsidya pa Mtsinje wa Ohio, pamene ine ndinali mlaliki wachinyamata wamng'ono pafupi usinkhu wa zaka makumi awiri ndi ziwiri, ndikuyimba imeneyo uko. Ndipo ine ndinamva, ndinayang'ana pamwamba pa ine, ndipo ndinamva Liwu likuti, “Yang'ana mmwamba.” Apa panabwera Kuwala kwakukulu kuja kutapachikika patalipo, kunabwera kukusunthira pansu pamwamba pa ine ndipo anati, “Monga Yohane Mbatizi anatumidwa kuti adzatsogolere kudza koyamba kwa Khristu, iwe ukhala ndi Uthenga womwe uti utsogolere Kudza kwachiwiri kwa Khristu.”

O, ine ndikanati ndikhulupirire chotani izo? Koma izo zinachitika chimodzimodzi basi. Ndipo usikuuno moto wa chitsitsimutso ukuyaka konsekonse ndi kuzungulira dziko. Mpingo waukulu wa Mulungu wolipidwira dipo unadzikweza Wokha kuchokera pa malo amenewo, ndi misonkhano yayikulu

ya machiritso, ndi zizindikiro, ndi zodabwitsa, ndi zozizwitsa, kuwonetsa pamenepo kudzako.

<sup>143</sup> Ndinu wobwera, ndipo ndinu mlendo. Inu mumachita zinthu zachirendo, zosiyana ndi zomwe inu munkakonda kuzichita. Inu simukuchita monga inu munkachitira. Anthu... Mzimu Woyera, pamene Iwo ubwera pa inu, ndipo inu mukakhala wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, inu mumazinyalanyaza zinthu za mdziko. Inu mumazinyalanyaza zinthu zimene zikanati zikufooketseni inu. Inu mumazinyalanyaza izo. Ndiye inu mumakhala cholengedwa chochita mo—mosamvetsetseka, bakha wonyansa, kwa iwo, mphungu yaying’ono yomwe inafungatiridwa pansu pa chisa cha nkhuu; imene ine ndinalalikira, *Ndipo Pamene Mphungu Ikasula Chisa Chake*. Ndinu cholengedwa chowoneka-moseketsa, kwa iwo.

Koma, o, mai, mukuyenda mu Msewuwaukulu wa Mfumu! Ameni. O, ndi Msewuwaukulu wa Kumwamba. Ndipo ine ndikuyenda chokwera nawo Msewuwaukulu wa Mfumu.

Akuti, “Tayang’anani pa woyera-wodzigudubuza uyo, bakha wonyansayo. Ndi mlaliki woyera-wodzigudubuza uja.”

<sup>144</sup> Mlaliki wotchuka wa Methodisti ananena kwa mwamuna lero, mu Louisville, anati, “Ine ndikanafuna kuti ndimuthandize M’bale Billy, koma inu mukudziwa chimene ine ndikanachita? Ine ndikanayenera kuti nditulutse khosi langa kunja.” Inu simukusowa kuti munditulutsire ine khosi lanu.

Iye anakoleka moyo Wake chifukwa cha ine. Ameni! ...?... Kumangoyenda chokweza Msewuwaukulu wa Mfumu, ndizo zonse. O, mai! Wodzazidwa ndi Mzimu Wake! Wobadwa ndi Mzimu Wake! Wotsukidwa mu Magazi Ake! Aleluya! Wokondwa!

<sup>145</sup> Ndiyeno chinthu china, bwanji, nchiyani chimakupangitsani inu kuchita zimenezo? Inu mukadali munthu, koma nchiyani chimakupangitsani inu kuchita zimenezo? Ndi chifukwa kuti inu munabwera, inuyo, Mzimu wanu unabwera kuchokera kumwamba. Ndi Mulungu mwa inu.

<sup>146</sup> Pamene ine ndinapita ku Roma, ine ndinazindikira kuti iwo, mmodzi aliyense, anali ndi mzimu wa Chiroma. Pamene ine ndinapita ku Greece, iwo onse anali ndi mzimu wa Chigriki. Ine ndinapita ku England; iwo onse anali ndi mzimu wa Chingerezi. Pamene inu mupita ku malo, inu mumakapeza... Ndiye inu mumakapeza mzimu wa Chimereka; ndi woyipa.

<sup>147</sup> Pamene ine ndinapita ku manda ogoba a San Angelo ku Roma, iwo anali ndi chizindikiro kumeneko, “Chonde, akazi Achimereka, valani zovala, kuti mulemekeze akufa.” Mzimu wa Chimereka.

Apenyeni iwo akamatsika ndege, ndipo atavala zovala zazing’onozo, ndipo aliyense amayamba kuyang’ana pa

iwo, ndipo apa pakubwera Abiti Amereka. Ndiwo mzimu Wachimereka. Inu mukhoza kudziwa kumene iye akuchokera; atavala, mnyamata, akukoka kagalu ka mphuno-yakuda kakang'ono kokalamba kumbuyo kwake. Ndiko kulondola. O, eya, iye ndi...Iye, iye ndi Wachimereka, Abiti Amereka; akuyenda pansu, inu mukudziwa, akudzitukumula monga choncho. Bwanji? Iye ali ndi mzimu wa Chimereka. [M'bale Branham akugogoda pa guwa kasanu ndi kamodzi—Mkonzi.] Koma Yesu anati, Iye anachitira umboni motsutsa izo tsiku limenelo, Iye anati, “Inu ndinu ochokera ku dziko ili lapansi. Ine ndine wochokera Kumwamba.”

Ndipo ngati inu muli nawo Mzimu wa Khristu mwa inu, ndinu wochokera Kumwamba, ndiye ndinu mlendo kuno.

<sup>148</sup> Koma inu muli ndi chikhalidwe cha malo amene inu mukuchokerako. Ndicho chimene ine ndikuyesera kunena. Mroma akabwera kuno, iye amakanda mutu wake; ndipo Mgermani akabwera kuno; Amereka akapita uko. Bwanji? Inu muli nayo mizimu ya maiko amenewo kumene inu mumachokerako.

Ndicho chimene chimatipanga ife osiyana kwambiri kwa dziko. Ndinu ochokera Kumwamba. Ndinu obadwa. Ndinu—ndinu mzika ya Ufumu wina. Inu mukukhulupirira zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi] Ndicho chimene Mzimu Woyera uli, ndi woti ukupangeni inu mzika ya Ufumu wa Mulungu.

<sup>149</sup> Ndiye, ngati ndinu mzika ya Ufumu wa Mulungu, kodi Iwo umakupangani inu kuchita motani? Monga Mulungu amachitira mu Ufumu Wake. Tsopano, kodi Mulungu amachita chiyani mu Ufumu Wake? Chiyero chake, chirungamo, ungwiwo wa lingaliro, ungwiwo wa maganizo; Mphamvu ndi chikondi, kupita kwa otayika, kuchiritsa odwala, kuchita zozizwitsa, kuchita zinthu zazikulu. Ndiye, kwa dziko iwe umawoneka wopenga, ndipo iwo amati, “Anyamata awa azungulira mitu.” Mwaona? Koma inu ndinu mzika ya Ufumu.

<sup>150</sup> Lemba linanso, ngati inu mukufuna kuti mulilembe ilo, Yohane 12:24. Ndiroleni ine ndikuwerengereni inu ilo mwamsanga kumene. Yesu anati:

...Ngati *mbewu ya tirigu* igwera mu *nthaka*...  
kupatula iyo ikafa, iyo siyingakhoze kubweretsa moyo wina.

Tsopano, penyani, chonena chimodzi chotsekera tsopano. Ndipo kumbukirani, ndiye, izo ziri mwamtheradi... Tsopano, kwa inu anthu, ziri mwamtheradi zoyenera ndi zofunikira, ndi kukakamiza ndi chikakamizo, kuti inu mulandire Mzimu Woyera tsopano. Pakuti, ngati inu simutero, inu simungakhoze kubwera mu chiwukitsiro. Tsopano penyani. Mulungu

sangakhoze kuswa malamulo Ake. Ife tikudziwa zimenezo. Iye amatsatira malamulo Ake.

<sup>151</sup> Tsopano, m—mbewu ya tirigu, kapena chimanga, ife titenga, monga Yesu ananena apo. Zoonā, m—mbewu, mu Baibulo, ine ndinali kungowerenga izo lero, akunena za thonje kapena mtundu uliwonse wa mbewu, koma, tirigu, barele, leizi, kapena chirichonse, ndi mbewu koma pamene mbewu ya tirigu igwera mu nthaka, tsopano pali . . . Tonse a ife pano taziwona, tikudziwa izi zimachitika. Mbewu ya tirigu, kapena njere ya chimanga, ikhoza kuwoneka mwangwiro monga iyo ingakhalire, ndipo inu mukayika iyo mu nthaka, ndipo ngati mbewu imeneyo . . .

Iyo ili nawo moyo wopitiriza. Iyo ipita pansi lero, kudzubala yokha mu phesi; ndi kubwereranso pansi, ndi kukwera mmwamba kachiwiri; ndi kubwereranso pansi. Ndi moyo wopitiriza.

Ngati mbewu imeneyo ilibe nyongolosi ya moyo mwa iyo, ziribe kanthu momwe iyo ikuwonekera mokongola, iyo siidzawuka konse. Iyo idzapita ku nthaka ndi kuvunda, ndipo ndi zomwezo. Gawo la iyo, zipangizo, zikhoza kugwiritsidwa ntchito ngati manyowa ndi zinthu mu nthaka. Koma kunena za iyo kukhalanso moyo, iyo siidzakhalanso moyo kupatula iyo itakhala nawo moyo wopitiriza mwa iyo. Aliyense akudziwa zimenezo. Inu simungakhoze basi.

<sup>152</sup> Pakhoza kukhala amuna awiri, mmodzi wa iwo chimodzimidzi basi, onse a iwo ofanana basi. Mmodzi wa iwo akhoza kukhala munthu wabwino, iye akhoza kumachita ntchito zabwino, iye akhoza kuchita zina zotero; koma kupatula munthu ameneyo ali nawo Moyo Wamuyaya mwa iye, iye sadzawuka konse mu chiwukitsiro. Iye sangakhoze kuchita izo; mulibe chirichonse mmenemo choti chimuwukitse. Mulibemo kanthu koti kamuwukitse iye, mulibemo Moyo. Kotero, inu mukuona, m'bale wanga wofunika, mlongo wanga wokonedwa, kupatula munthu akabadwa kachiwiri, iye sangakhoze mwanjira iliyonse kubwereranso mu Ufumu uwu. Iye sangakhoze. “Kupatula Mbewu ya Tirigu iyi ikagwera mu nthaka ndi kufa.” Iye anali kuyankhula za Iyemwini. Koma Iye anali nawo, osati moyo wopitiriza, Iye anali nawo Moyo Wamuyaya; ndipo Moyo umenewo Iye anawupereka kwa inu, kuti inu mukhoze kukhala nawo mtundu womwewo wa Moyo.

<sup>153</sup> Tsopano, ngati inu mutangokhala ndi moyo waumunthu, wokwanira kuti uzikuyendetsani inu ponseponse ndi kumakhumbira, “Iye amene akhala mu zosangalatsa ali wakufa pamene akadali wamoyo,” iwe sungakhoze kuwuka. Iwe ukhoza kukhala msungwana wotchuka kwambiri pa sukulu. Iwe ukhoza kukhala msungwana wotchuka kwambiri pa masewero a juga ya ku gulu lanu. Iwe ukhoza kukhala mkazi wovala bwino mu dziko. Iwe ukhoza kukhala wokongoletsetsa. Iwe ukhoza

kukhala womangidwa bwino kwambiri. Iwe ukhoza kukhala fano kwa mwamuna wako. Iwe ukhoza kukhala zinthu zonse izi, zimene, zomwe ziri zodabwitsa. Koma, mlongo, kupatula iwe utakhala nawo Mzimu Woyera mwa iwe, umene uli Moyo Wamuyaya, pa mapeto a msewu uno iwe watha.

Ndipo ine sindikusamala momwe iwe umawonekera kapena momwe zinthu izi ziliri, kapena momwe iwe uliri wosatchuka kapena wotchuka, momwe iwe uliri wokongola kapena momwe uliri wosakongola; ngati iwe uli nawo Moyo Wamuyaya, uko iwe ukakhala kwa nthawi za nthawi.

<sup>154</sup> Pamene mwezi ndi nyenyezi zikakhala zitachoka, ndipo dziko lapansi ladzilirira lokha mpaka ku mapiri ndi zipululu, ndi chirichonse chiri—chiri nacho, palibenso; ndipo dziko litazandima ngati munthu woledzera akubwera kunyumba usiku, ndipo nyenyezi zitakana kuwala, ndi kugwa kuchokera mmiyamba, ndipo mwezi ukusandulika magazi; ndipo—dzuwa nkuchita manyazi ndi kubisa nkhope yake, pamene iwo awona Mwana wa munthu akubwera. Inu mudzawala mwa chirungamo cha Yesu Khristu, mukutuluka kuchokera ku manda ngati mkazi, wamng’ono wokongola, kuti mukatengane ndi mwamunanu, ndi kukakhala kwa nthawi za nthawi ndi nthawi za nthawi ndi kwa nthawi za nthawi, ndipo mibadwo yonse Yamuyaya inu muzikakhalabe moyo. Ndicho chimene Mzimu Woyera unaperekedwera.

Ngati inu mukumverera kukoka kwakung’ono, musati muwuthamangitse Iwo.

<sup>155</sup> Kodi Mzimu Woyera ndi chiyani? Mulungu mwa inu. Kodi Iwo ndi wachiyani? Kuti upitirize ntchito Yake pakati pa anthu Ake; kuti uwubweretse Mpingo Wake palimodzi, kuti uwubweretse Mpingo pa malo mu tsiku lino, patali kuposa Achilutera, Amethodisti, ndi Achipentekoste, kupita mu malo a kukhazikitsidwa ndi chisomo Chokwatulitsa. Kuti, pamene gawo ili la Mpingo, pamene Mzimu usunthira mu Mpingo uwu pano, iwo udzangowuka; ndipo iwo udzabweretsa, kubweretsa owomboledwa onse omwe anawukhudza Mzimu umenewo.

Achilutera aja amene anayima pamenepo ndi kuwala konse kumene iwo anali nako, mu kulungamitsidwa; Amethodisti aja omwe ankagwera pansu, ndipo iwo ankaponyera madzi mu nkhope zawo, pamene Mzimu unawakhudza iwo kupyolera mu kuyeretsedwa; Achipentekoste aja, omwe ankayenda chokwera-ndi-chotsika mu msewu ndipo ankawatcha iwo “odukamalirime, kapena obwebweta ndi chinenero cha abakha,” ndi zonse izo; iwo adzayima mu chirungamo, pamaso pa Mulungu pa Tsiku limenelo, moonu basi monga Baibulo ili layima pano. Ngati inu mukundikhulupirira ine kukhala wantchito... Inu mumanditcha ine mneneri Wake; ine sindimadzitcha ndekha zimenezo. Koma, inu mvetserani, ine ndikukuuzani inu mu

Dzina la Ambuye. Iwo amene ali mwa Khristu Mulungu adzabwera nawo ndi Iye pa kudza Kwake, pa chiwukitsiro, ndipo okhawo amene ali mwa Khristu.

Mumalowa chotani mwa Khristu, anthunu?

<sup>156</sup> Mwa chikhulupiriro chimodzi ife tonse timalumikizidwira mkati? Ayi. Mwa chanza chimodzi ife tonse timakokedwera mkati? Ayi. Mwa madzi amodzi ife tonse timabatizidwira mkati? Ayi. Kapena mwa chipembedzo chimodzi ife tonse timapangidwira chipembedzo mkati? Ayi.

Koma, mwa Akorinto Woyamba 12:13, “Mwa Mzimu umodzi, Mzimu Woyera, Mzimu wa Mulungu, ife tonse tiri. . .” Amethodisti, Abaptisti, Achilutera, Apresbateria, “Timayenda mu Kuwala, monga Iye ali mu Kuwala, ife timakhala nacho chiyanjano wina ndi mzake, ndipo Magazi a Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu, amatitsuka ife kuchoka ku kusalungama konse.” “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi, ndipo tapangidwa ogawana nawo a chisomo Chake.”

<sup>157</sup> Inu simungakhoze kupita ku Chiweruzo. “Iye amene amva Mawu Anga ndi kuwakhulupirira.” Palibe munthu angakhoze kukhulupirira mpaka iye atakhala nawo Mzimu Woyera. “Ndi kukhulupirira pa Iye amene anandituma Ine,” pamene Mzimu Woyera wachitira umboni za chiwukitsiro Chake. “Ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzabwera konse ku chiweruzo, koma wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.” Chiyani? Inu simudzakhudza konse Chiweruzo. Inu simudzayima konse pa Mpandowachifumu Woyera kuti muweruzidwe.

Inu mumakomana nacho chiweruzo chanu komwe kuno. Inu mumadutsa chiweruzo chanu pamene inu mudutsa ndi kuti, “Ine sindine wabwino, ndipo kuphunzira kwanga si kwabwino. Ambuye, bwerani mkati mwa ine, ndipo nditengeni ine ndipo munditsogolere ine, Ambuye. Ine sindikusamala chimene dziko lopenga ili likunena. Nditsogolereni ine, Ambuye, ndi Mzimu Wanu.” Iwe waweruzidwa pamenepo. Dziweruzeni nokha ngati wopusa chifukwa cha Khristu, ndipo, mu chirungamo Chake, Tsiku limenelo ife tidzayima mwachisavundi mu mawonekedwe Ake.

<sup>158</sup> Njira imodzi yokha. Motani? “Mwa Mzimu umodzi ife tonse timabatizidwa kulowa mu Thupi limodzi.” Ndipo pamene inu muli mu Thupi limenelo, chiweruzo chaweruzo kale Thupi limenelo, ndipo inu mwamuvomereza Iye ngati chitetezero cha tchimo lanu.

Inu mukuti, “Ine ndachita zimenezo, M’bale Branham.”

Ndiye, ngati Mzimu Woyera wabwerera ndi kukupatsani inu chisindikizo ngati chizindikiro, Mzimu umenewo umakubweretsani inu kulowa mu Thupi la Khristu. Inu mumatembenukira ku njira yina, ndipo ndinu cholengedwa

chatsopano mwa Khristu Yesu. “Inu mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Zinthu zakale zapita, ndipo inu ndinu watsopano mwa Khristu!” Amen!

<sup>159</sup> O, chonde, ndiroleni ine ndikukakamizeni inu, m’bale wanga wa Chikhristu kapena mlongo. Musati mulole chitsitsimutso ichi chikudutseni inu. Inu muyenera kulanjira Mzimu Woyera. Ndi chiyani Iwo? Mzimu wa Mulungu. Kodi Iwo unali wa chiyani? Kuti ukutsogolereni inu, kukulondolerani inu, kukudzazani inu, kukuyeretsani inu, kukutulutsani inu, kulowa mu Mpingo.

Kodi mpingo ndi chiyani, kodi mawu akuti *mpingo* amatanthauza chiyani? “Otulutsidwa, olekanitsidwa.” O, momwe ine ndingakhazere kutenga ulaliki kuchokera pamene pakali pano! “Otulutsidwa, olekanitsidwa,” alendo, akutali ndi dziko, mwendamnjira ndi mlendo, kudzinenera kuti ife tiribe kuno mzinda wapadziko umene ife tikukhumba kuti tizikhalamo. O, mai!

<sup>160</sup> Monga Abrahamu, ndi Isaki, ndi Yakobo, anayenda, akukhala mu mahema mu dzikolo. Iwo ankadzinenera kuti iwo anali amwendamnjira ndi alendo, mbewu ya olowa, olowa kale uko; kholo, wolowa. Ife ndife mbewu zawo. “Ndipo iwo anali akufunafuna Mzinda Umene Wowumanga wake ndi wowupanga anali Mulungu.” Amen. Iwo anali akuwufunafuna.

<sup>161</sup> Ndipo, lero, mbewu yawo ikadafunafunabe Mzinda wakudza, akuti, “Ine sindikufuna kusinthidwa monga mwa dziko ili. Ine sindikufuna kanthu kochita nalo dziko ili. Ine ndikufuna, ine ndikufunafuna Mzinda womwe wamangidwa mwa mphwamphwa. Ine ndikufunafuna Mzinda umene uli nawo Moyo Wamuyaya, kumene dzuwa silidzalowa konse, kumene sikudzakhala konse usinkhu waukalamba, kumene sikudzakhala nkhatu yachisoni pa chotsegulira chitseko, kapena manda ku mbali ya phiri. Ine ndikufunafuna Mzinda umenewo, Umene Wowumanga wake ndi Wowupanga, ali Mulungu.”

<sup>162</sup> Pali njira imodzi yokha kuti uwupeze iwo. “Panali Mwala umene unadulidwa kuchokera ku phiri, popanda manja, umene unagudubuzikira mu dziko ndipo unaliphwanya ilo, ndipo ilo linasanduka ngati tirigu. . . kapena mungu pa dwale lopunthira.” Mulole Mwala umenewo, Khristu Yesu; Mwala-wopunthwitsa uja kwa dziko, Mwala wodedwa, Mwala-wosekedwa, chinthu-chopunthwitsa kwa mpingo; koma wodula ndi Mwala-wachikoka kwa wokhulupirira, Mwala wa chitsimikizo, Mwala wa mpumulo. O, mai!

Kupumula! Ine ndikudziwa kuti ine ndadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Moyo wanga uli pa mpumulo. O! “Bwerani kwa Ine nonse inu mukuvutika ndi olemedwa kwambiri, ndipo Ine ndidzakupatsani inu mpumulo kwa moyo wanu.” “Chi—chizindikiro chimene chiti chidzanenedwere moyipa,” anatero—mneneri kwa Maria. Icho chidzakhala chizindikiro,

zedi, icho chidzakhala. Koma Icho chidzakhala chitsimikizo. Icho chidzakhala chikondi. Icho chidzakhala chokhutitsa. Icho chidzakhala chinachake chimene iwe ungadziwe kuti iwe wadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo.

<sup>163</sup> M'bale wanga, mlongo wanga; ngati m'bale wanu, ngati wantchito wanu mwa Khristu, ndiroleni ine ndikukakamizireni inu, monga ndi mtima wanga wonse. Musati mulole izi zikudutseni pamwamba pa mitu yanu, kapena kukulambalalani inu, kapena pansu pa inu. Landirani Iwo mu mtima wanu, ndipo inu mukhala munthu wokondwa pa dziko lapansi.

Ine sindiri kukulonjezani inu kuti mupeza madola milioni. Ayi, bwana. M'bale Leo, ine ndikuganiza pakhala zambiri za izo zikulonjezedwa tsopano, “mamilioni a madola,” zinthu zimene osiyana ena amati. “Ngati iwe uti ukhale Mkristu, iwe upeza mamilioni a madola ndipo iwe ukhala munthu wolemera.” Ine sindiri kukulonjezani inu kanthu.

Ine ndikukulonjezani inu ichi, chinthu chokha chimene ine ndingakhoze kukulonjezani inu, chipulumutso Chake. Chisomo Chake ndi chokwanira kwa yesero lililonse. Anthu a pa Pentekoste, iwo sankafuna ngakhale chimene iwo anali nacho. Tsopano nkumanena za amamilioni? Iwo sankazifuna zimene iwo anali nazo, Mlongo Angie.

<sup>164</sup> Ine ndikufuna ndidzakumveni inu ndi Gertie mukuyimba, limodzi la masiku amenewa, (kodi ali pati iye?), *Sabata yobwera Kwathu*, limodzi la masiku amenewa. Ambiri a iwo awoloka kale malire chiyambireni chija. O, mai!

Iwo sanapemphe zinthu zazikulu. Iwo sanapemphe ndalama. Bwanji, Petro anati, “Siliva ndi golide ine ndiribe, koma chimene ine ndiri nacho, ine ndipereka icho kwa iwe.”

Ndipo ine ndikunena chimenecho usikuuno, amzanga. Chimwemwe, chikondi, chitsimikizo, chimene ine ndiri nacho cha Khristu ndi chiwukitsiro Chake, chimene ine ndiri nacho, ine ndikupereka kwa inu; ine ndikupereka kwa inu, ngati ana a Mulungu.

Ndipo inu mubwere ndi kudzakhala pa mtanda ngati Mulungu anakuyitanani inu, ndipo musati munyamukepo. Pamene muzibwera mawa usiku, inu mudzabwere kapena kuti mudzalowe mkati muno ndi kudzakhala mpaka izo zitatha; kapena mudzabwerepo ndipo ife tidzapemphera ndi kusanjika manja pa inu. Pitani. . . Ndilo dongosolo la Baibulo, kusanjika manja pa iwo kuti alandire Mzimu Woyera. Ndiyeno ife tikuti, inu mupite ku nyumba yanu. . . Ngati inu muti mukhale pomwepo, ngati inu muti mukhale usiku wonse, mukhale tsiku lotsatira, kukhala tsiku lotsatira, kukhala kupyola tchuthi, kukhala mpaka kuyamba kwa chaka, ndipo khalanibe, mukhale mpakana.



<sup>165</sup> Kuti, chirichonse chimene ife titi tikulangizeni mawa usiku, kukusonyezani inu mu Baibulo chimene chiyenera kuchitika, chidzabwera. Ndipo pamene Iwo ubwera, ndiye palibe adierekezi okwanira mu kuzunzika... Inu mukudziwa inuyo mwadutsa kuchokera ku imfa kupita ku Moyo. Ndinu cholengedwa chatsopano mwa Khristu Yesu. Mabelu achimwemwe a Kumwamba azidzayimba.

<sup>166</sup> M'bale Othal, ine ndikukuuzani inu, izo zimangokuyika iwe pa moto. Apa pali mnyamata wachikulire wakhala apayu, m'bale wachikulire wa ine, yemwe anali wachifwamba akuyenda ndi mifuti pa mbali yake, akufunafuna munthu pa ngodya, winawake woti awombere ubongo wawo utulukemo. Ndipo nchiyani chinachitika? Tsiku lina iye anayang'ana ndipo anakhulupirira kumka ku Moyo. Ndipo iye anayenda mopitirira. Iye amatsatira misonkhano yanga. Ndipo munthu wosaukayo, wopanda zokwanira kuti azidya, ndipo ankadzilambatika nagona mu matchire pambali pa hema, ali wa njala ndi waludzu. Ndipo tsiku limodzi Mzimu Woyera unabwera. O, m'bale wanga, iwo unakusintha iwe, sichoncho? Iwo unabweretsa Moyo, ndipo anachotsamo imfa. Udani unachoka, ndipo chikondi chinabwera mkatimo. O, mai! Udani ndi makangano zonsezo zinagwera kutali; Moyo watsopano unabwera mkati.

Penyani apa pa ena kuphatikiza ena, ena kuphatikiza ena, ndi kunja kupyola uko. O, mabelu achimwemwe a Kumwamba akuyimba! Amzanga, palibe njira yoti ine ndifotokozere izo.

<sup>167</sup> Mvetserani, kuti ine ndikhoze kusiya izi, ngati inu mwaukhulupirira umboni wanga, ngati wantchito wa Khristu, ndipo ndayesera kukusonyezani inu kuchokera mu Baibulo la Mulungu kuti ndi zolondola. Ndipo ngati mawu anga awoneka ngati angakhale odabwitsa pang'ono pa izi, tayang'anani pa chithunzi chija mu dziko lasayansi. Penyani chipatso, chomwe Lawi la Moto ili limene linatsogolera Ana a Israeli, penyani chipatso chimene Ilo likubala. Onani chimene Ilo likufotokoza, chimene Ilo likunena.

Si ine amene ndimayankhula; ndi Iye amene amayankhula kupyolera mwa inu, inu mukuona. Si ine amene ndimawona masomphenya; ndi Iye amene amayankhula kupyolera mwa inu. Si ine ayi amene ndimachiza odwala; ndi Iye yemwe ali mwa inu, amachiza odwala. Si ine amene ndimalalikira; ndine wamantha wobwerera mmbuyo, ndi wothawa pa lingaliro lomwe, koma ndi Iye yemwe amayankhula kupyoleramo. Ine sindimawadziwa Mawu; koma Iye amawadziwa Iwo. Ndi zimenezo. Ndi zimenezo. Ndizo zomwe izo ziri.

Ndipo ndi Uyo apo. Ndipo Mngelo yemwe uja wa Mulungu ali pomwe pano mu nyumba ino usikuuno. [M'bale Branham akugogoda pa guwa—Mkonzi.] O, momwe ine ndikumukondera Iye!

168 Tsopano ndi angati akufuna kuti alandire Mzimu Woyera? Tengani kufufuza kwa miyoyo yanu. Ndi angati amene sanaulandire Iwo, ndipo akufuna kutero? Kwezani mmwamba dzanja lanu, nenani, “M’bale Branham, mwakuya kwa mtima wanga, ine ndikufuna kuti ndilandire Mzimu Woyera.” Mulungu akudalitseni inu, paliponsepo.

169 Ndi angati a inu amene munalandira Iwo, ndipo mukufuna kuti muzipita monga iwo ankachitira mu Machitidwe 4, ndi kuti, “O Ambuye, O Ambuye, tambasulani dzanja Lanu kuti muzichiza, ndi kusonyeza zizindikiro ndi zodabwitsa mu Dzina la Mwana Wanu Yesu woyera, ndipo mundipatse ine kulimbantima konse ndi chikondi, kuti ndiziyankhula, ndi kudzaza kwatsopano”? Inde, pano pali wanga, inenso. Mulungu, perekani Iwo kwa ine.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu, mwa kuya kwambiri kwa kuonamtima, munthu aliyense atagwirizira chokhumba chanu mu mtima wanu.

170 Ambuye Yesu, ife tikutseka kusunkhana kwakung’ono uku usikuuno, chitatha chiyanjano cha pozungulira Mawu ndi Mzimu Woyera. Momwe Iye watidalitsira ife ndi kutsanulira mu mitima yathu mafuta a Mawu Ake! Muli azitumiki, muli amuna muno amene anali mu mayendedwe onse a moyo, omwe analawa ndipo anawona kuti Ambuye ndi abwino. Ife tikudziwa chimene Mzimu Woyera uli tsopano, lonjezo la Mulungu. Iwo uli Moyo Wamuyaya kwa onse amene akhulupirira.

171 Ndipo ife tikudziwa kuti Mzimu Woyera unali Mzimu wa Yesu Khristu utatumizidwanso, ndipo Iye ali mwa ife lero. Monga Mulungu anali pamwamba pa ife, mu Lawi la Moto lija; ndiye Iye anayenda ndi ife, mu . . . thupi limene linkatchedwa *Emanuele*, “Mulungu nafe”; ndipo tsopano Iye ali mwa ife, mwa Mzimu Woyera, Mulungu mwa ife. O!

Yesu anati, “Pa tsiku limenelo inu mudzadziwa kuti Ine ndiri mwa Atate, ndipo inu muli mwa Ine, ndipo Ine ndiri mwa inu. Inu mudzamvetsa izo tsiku limenelo. Chifukwa, inu muli mu dziko la mdima, monga tinganenere, tsopano, koma pa tsiku limenelo inu mudzamvetsa.”

172 Atate, izo sizikanakhoza kupangitsidwa kumveka ndi mwangwiro, chifukwa ndiye ife tikadakhala opanda chinthu choti tikhaliire nacho chikhulupiriro. Koma ntchito zonse za Mulungu ziri zolamuliridwa mwa chikhulupiriro. Ndipo mwa chikhulupiriro mu Mawu Anu, mwa umboni wa Mzimu Woyera umene ife tikudziwa tsopano, ine ndikupempha kuti moyo uliwonse wanjala mkati muno udzadzazidwe ndi Mzimu Woyera. Iwo amene alibe Iwo, ndipo akumva njala yofuna Iwo, ingokumbukirani. . . Ife tikananana kwa iwo, Ambuye, monga chonchi zimene Inu munanana, “Odala muli inu pamene muchita njala ndi ludzu. Inu mudzadzazitsidwa.” Ndilo lonjezo.

Ndipo ziri ngakhaleenso zodalitsidwa kukhala wanjala. Ndinu wodala ngakhale kudziwa kuti Mulungu wayankhula kwa inu, pakuti Iwo unati, “Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine kupatula Atate Anga atamukoka iye poyamba.”

<sup>173</sup> Ndipo, Ambuye, iwo amene ali ankhondo akale pano, iwo anakweza manja awo. Ine ndinakweza langa. O Ambuye, tipatseni ife nyonga, tipatseni ife Mphamvu kuti tikatambasule dzanja la Mwana Wanu woyera Yesu, kuti zizindikiro ndi zodabwitsa zikhoze kumachitidwa, kuti iwo ukakhale utumiki wakuya mochulukira, chinthu chachikulupo chomwe chinayamba chachitikapo. Tipatseni ife kulimbamtima ndi chikondi, kuti tiziyankhula kwa anthu. Perekani izo, Ambuye. Khalani nafe mu zinthu zonse, ife tikupempha mu Dzina la Yesu.

<sup>174</sup> Ndipo mawa usiku, Ambuye, mulole pabwere nkokomo wotero wa mphepo yamphamvu yamkuntho, ukugwera mu nyumba ino, kuti izo zidzangokhala ngati Tsiku lina la Pentekoste. Maziko ayikidwa kale. Chirichonse chiri chokonzeka. Ngombe zaphedwa, zonenepa zaphedwa, anaankhosa aphezwa; kama wakonzedwa, alendo ayitanidwa. O Ambuye, tumizani phwando la Pentekoste, mawa usiku, mu nyumba ino, ndipo dzazitsani moyo uliwonse ndi ubatizo wa Mzimu Woyera. Perekani izo, Atate. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amenii.

. . . tidzaphunzira zinthu zambiri,  
Tidzakhala ndi zeze wopangidwa ndi golide,  
mwina wa nsambo chikwi;  
Tidzayimba ndi kufuula ndi kuvinavina,  
mwanawankhosa adzawumitsa misonzi  
yathu;  
Tidzakhala ndi khomo limodzi-. . . sabata  
labwino la kubwera kwathu, zaka zikwi  
khumi zoyamba. Amenii!

Magazi ofunika a Mwana wa Mulungu Yemwe  
atsuka ndi kutiyeretsa  
Anthu odabwitsa chifukwa cha Dzina Lake  
ndipo akutchedwa Mkwatibwi.  
Ngakhale kuno okanidwa ndi onyozedwa,  
tsiku limodzi Ambuye adzabweretsa  
Osankhidwa mkati mwa chipata, ndipo ndi  
zoyenera chirichonse.

Tikadzakhala mkati mwa zipata za ngale,  
tidzaphunzira . . .



*Kodi Mzimu Woyera Ndi Chiyani?*

*(What Is The Holy Ghost?)*

Disembala 16, 1959, Lachitatu usiku

*Kodi Mzimu Woyera Unaperekedwera Chiyani?*

*(What Was The Holy Ghost Given For?)*

Disembala 17, 1959, Lachinayi usiku

Mauthenga awa a William Marrion Branham analalikidwa mu Chingerezi ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A. Kuyesa kulikonse kwachitidwa kuti timasulire molondola Mauthenga oyankhulidwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito kuti adindidwe pa tsamba, ndipo adindidwa ndi kugawidwa mopanda kugulitsa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1997 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE

P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS

P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)